
**BAPTIST PUBLISHING HOUSE**
**P.O. Box 416 Broken Hill,**
**ZAMBIA**
3d

FILE COPY 1965



## CIBVUMBULUTSO NDI KUDZA KWA AMBUYE

Buku la Cibvumbulutso ndi limodzi la mabuku odabwitsa a mBuku Lopatulika. Koma likhoza kukhala limodzi la mabuku osokoneza. Ndi buku limene tipeza zifanizilo zambili. Anthu amene analandila bukuli anazindikila tanthauzo la zifanizirozi. Cifukwa cace, anazindikila za buku ili ndi mau ace olimbikitsa. Mzimu Woyera unatsogolera Yohane kulemba buku ili lotsiriza la Buku Lopatulika panthawi imene aKristu anali kupatsidwa mlandu. Ambili anali kuphedwa. Anayenera kukhala osalimbikitsidwa ndi kudabwa cifukwa ninji Mulungu sanacitapo Kanthu kuwathandiza. Ngakhale Kuti sitikhoza kudziwa zonse za zifanizirozo, pali cimodzi codziwika kwambili. Ambuye adzabwela ndi mphamvu; Satana ndi iwo omtsatira adzaonongedwa m'nyanja ya moto wosatha. Iwo amene akonda ndi ku khulupirila Ambuye Yesu adzakhala ndi Iye m'moyo wosatha kumene kulibe cisoni, matenda, ndi imfa.

Cimo liri lotizungulira, koma tisafoke. Ngati tili a Kristu, tidziwa Kuti adzadza ndipo tidzanka naye mu ulemelero wace m'mwamba.

-ooOoo-



# BAIBULO - COTITSOGOLERA

Omasurila - N.M. Phiri

## MAKONZEDWE A BAIBULO


Page

MAU OTSEGULA: MA BAPTIST NDIWO ANI? ........... 1
MA BAPTIST AMAKHULUPILIRA CIANI? . 3

ULAMULIRO WA BAIBULO

WOLEMBA: NORMAN WOOD

PHUNZIRO

1 BAIBULO YATHU - NDICIANI? ............ 5
2 BAIBULO YATHU - TIDZIWA BWANJI KUTI NDIYOONA ............ 9
3 BAIBULO YATHU - MAU ACE APAKATI ....... 13
4 BAIBULO YATHU - IMALANKHULA KWA IFE LERO .................. 17

KUFUNA-FUNA NDIKUGWILITSA NCHITO BAIBULO YATHU


WOLEMBA: DUTTON BONNELL

5 MAGAWO AWIRI ENI-ENI A BAIBULO YATHU NDIZIMENE AMAPHUNZITSA .............. 21
6 MPHATSO YA MULUNGU ................. 25
7 KUFUNA-FUNA MU BAIBULO PANGANO LACE NDI MPHATSO ZACE - MBALI YOYAMBA .... 28
8 KUFUNA-FUNA MU BAIBULO PANGANO LACE NDI MPHATSO ZACE - MBALI YACIWIRI .... 31

UTHENGA WA BAIBULO

WOLEMBA: TOM SMALL

9 CIYAMBI CACE ......................... 34
10 KUKHALA MU DZIKO LALONJEZANO ........ 38
11 KUBWERANSO KWA MPULUMUTSI WATHU .. 43
12 MAYAMBIDWE A MA CHALICHI OYAMBA .... 47
13 KUBWERANSO KWA KRISTU ............... 51




mutsidwa pamene Ambuye abwelanso? Mpingo waku Tesalonika unali kudabwa pa ici. Kupyolera mwa Mtumiki Paulo, Mulungu anawauza Kuti, pabwela kwa Ambuye, "Akufa mwa Ambuye adzauka poyamba: ndipo ife amoyo otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga: ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse." 1 Atesalonika 4:16b,17.

Mu 2 Atesalonika 1:7b-9 tauzidwa za masautso ndi cilango kwa iwo amene sanalape ndikukhulupirila Kristu ngati Mpulumutsi wao: "Pa bvumbulutso la Ambuye Yesu wocokera Kumwamba pamodzi ndi Angelo a mphamvu yace, m'lawi la moto, ndi kubwezera cilango kwa iwo osamdziwa Mulungu, ndi iwo osamvera Uthenga Wabwino wa Ambuye Wathu Yesu: amene adzamva cilango, ndico ciononqeko cosatha cowasiyanitsa kunkhope ya Ambuye, ndi kuulemelero wa mphamvu yace."

## CIKONZEKERO CA KUDZA KWACE

Anthu ambili amakhala nthawi yaitali kuyesa kulota nthawi imene Ambuye adzabwela. Uku ndiko kutaya nthawi pacabe. Buku Lopalulika silitiuza. Ophunzila anafuna kudziwa, ndipo anafunsa Yesu zaici pamene asanakwele kumwamba. Yesu anawauza, "Sikuli kwa inu kudziwa nthawi kapena nyengo, zimene Atate anaziika m'ulamuliro wace wa Iye yekha. Macitidwe 1:7.

Cinthu cacikulu sikunena kuti "Kodi Ambuye adzabwela liti?" Koma "Kodi ndidzakonzekera bwanji Kubwela kwace?" Kuli njila imodzi yokonzekera kwa munthu amene asanapulumutsidwe. Ayenela kulapa zocimwa zace ndiku bvomeleza Yesu kukhala mpulumutsi wace. Munthu amene akana kulapa zoipa zace ndikukhulupirila Yesu sakhoza kukonzekera kudza kwa Ambuye. Ngati mKristu afuna kukonzekera kudza kwa Ambuye, ayenera kucita cifuniro ca Yesu tsiku ndi tsiku. Versi lotsiliza la phunzilo lathu linena kuti: "Momwemo, okondedwa, popeza muyembekeza izi, citani cangu Kuti mupezedwe ndi Iye mumtendere, opanda banga ndi opanda cirema. 2 Petro 3:14.

akumbutsa a Kristu zinthu ziwiri. Coyamba cipezeka mu versi 7. Mau osasinthika omweo, amene analonjeza mvula m'masiku a Nowa alankhulidwa. Auza anthu Kuti Ambaye adzabwelanso kudzaweruza dziko lapansi. Tsiku lina Ambuye adzabweradi.

Caciwiri cimene aKristu akumbutsidwa naco ndico Kuti Mulungu sawerenga nyengo monga ife timawerenga. Anthu amanena, "Papita nthawi yaitali kucoka pamene Yesu anafa, ndikuuka kwa akufa, ndi kukwela kumwamba." Inde, m'malingiliro a munthu yakhala nthawi yaitari. Koma tauzidwa, "Tsiku limodzi likhala kwa Ambuye ngati zaka cikwi, ndi zaka cikwi ngati tsiku lomodzi." 2 Petro 3:8b.

## KUSADZIWIKA KWA NYENGO YAKUBWERANSO KWACE

Ngakhale tidziwa Kuti Ambuye adzabweranso, sitidziwa ndi liti adzabwela. Versi 10 litiuza Kuti "Koma tsiku la Ambuye lidzadza ngati mbala nthawi yausiku." 2 Petro 3:10a. Sanena Kuti Ambuye adzadza ngati mbala usiku. Anena Kuti: Monga mbala idza pamene eni nyumba sayembekeza Kuti idzadza, momwemonso Ambuye adzabwela pamene anthu samuyembekezera kufika. Kukamba zakubweranso Kwace, Yesu anati, "Koma za tsiku ilo ndi nthawi yace sadziwa munthu ali yense, angakhale angelo a Kumwamba, koma Atate yekha." Mateyu 24:36.

Timawerenga cifukwa cace Ambuye alinkucedwa kubweranso. Kwace "Ambuye sazengereza nalo lonjezano, monga ena aciyesa cizengelezo; komatu aleza mtima kwa inu, wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike Kukulapa." (versi 9). Ciri cifundo ca Ambuye cimene cicedwetsa Kubwela kwace. Afuna kupatsa munthu ali yense mwai wakulapa ndi kupulumutsidwa.

## ZOCITIKA PAKUDZA KWACE

Ncosatheka kunena mau onse amene atiuza zimene zidzacitika pakubwela kwa Ambuye. Pali zinthu zina zimene tiyenela kukamba mwatsatanetsatane.

Coyamba ndi ici: Cidzacitika ndi ciani kwa opulu-



# MA BAPTIST NDIWO ANI?

Pazipatso zao mudzawazindikira iwo. Mateyu 7:20.

Mu caka ca 1962 kucuruka kwa anthu a Baptist padziko lonse la pansi anali okwanira zikwi makumi awiri ndizisanu (25 million). Unyinji woterou ndi akuru - akuru okha osati ana ai. Gulu imeneyi ndi okha anthu amene anakhulupilira Ambuye Yesu Kristu kuti ndi mpulumutsi wao ndikugwirizana ndi church yapamudzi pao.

Ku dziko la America kuli ma Baptists kucuruka kwao zikwi makumi awiri ndicimodzi (21 million). Mugulu imeneyi zikwi khumi ndi a ku mwera kwa America. Ma Baptist a ku mwera ndilo gulu yaikuru ndiyamphamvu mu dziko la America. Kuli ma church opyola zikwi makumi atatu ndi asanu (35 thousand) ma church amenewa ali ogwilizana ndi Baptist Mission ya muno mu Zambia. Ma Baptist a ku mwera ali ndi nchito ya Mission mumaiko okwanira makumi asanu ndi atatu (35 countries) pa dziko lonse la pansi ndipo ali nao mamishonare oposa cikwi cimodzi ndi makumi asanu ndi atatu ndipo ali kuuza uthenga wacipulumutso pa dziko lonse lapansi.

Mu AFRICA muli anthu okwanira zikwi mazana atatu kudza makumi asanu ndi awiri ndi anthu asanu ndi modzi (376 thousand). Kuli ma church a Baptist kucokera ku mpoto kufikira ku mwera kwa dziko lathu Africa. Ma Baptist ku Malawi, Southern Rhodesia, ndi muno mu Zambia ali ocuruka kokwana zikwi zisanu ndi zinai ndipo kucuruka kwa anthu kuli kuonjezekera tsiku ndi tsiku. Baptist yaku mwera ili ndi cipatala ndi sukulu ku Sanyati, nyumba yosindikiza timabuku ku Bulawayo, sukulu ya Abusa ku Gwelo, ndima church ambiri.

Muno mu ZAMBIA muli ma Baptist Church ku Lusaka, Broken Hill, Kitwe, Ndola, Luanshya, Chingola ndi ku Mufulira. Baptist Mission ya muno mu Zambia ili ndi nyumba yosindikiza timabuku mu Broken Hill. Ali kuganiza kumanga nyumba ya Baptist ku Lusaka m'mene mudzakhala, zipinda zosindikiza, zipindi za waelesi, ndizipinda za ofuna kuphunzira mau a Mulungu otumizidwa.

Mulungu anadalitsa gulu la Baptist cifukwa amalalikira uthenga ndikufuna-funa otaika adze kwa Kristu ndikuwaphunzitsa makhalidwe acikristu. Mulungunso adalitsa gulu ili cifukwa imakhulupilira ndikucita ziphunzitso za cipangano catsopano.

Ma Baptist amafuna-funa kumvera LAMULO LALIKURU la Ambuye lakuti:

> "Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndikuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzima Woyera ndikuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu, ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimariziro ca nthawi ya pansi pano."
>
> Mateyu 28:19,20.

## DZINA LOTI "BAPTIST"

Ma Baptist sakhoza kudziwa ciyambidwe cao monga magulu ena. Anthu ena amadodoma kuti ma Baptist anatenga dzina lao kucokera kwa Yohane Mbatizi amene anenedwa mu cipangano catsopano, koma ma Baptist sanatenge dzina lao kucokena kwa Yohane Mbatizi. Tiyenera kukumbukira kuti, ngakhale dzina loti "Baptist" siinapatsidwa kufikira zaka mazana ocepera apitawa ndi adani a ma Baptist, Ma Baptist zolinga zao ndizocita zao zakhala kwa zaka mazana - mazana apitawa mu nkhani za akrisitu. Anthu amene aitanidwa "Ma Baptist" lero anali kuitanidwa "Anabaptists" cimene cinena "amene amabatizanso." Dzina ili anapatsidwa ndi adani a ma Baptist cifukwa camacitidwe ao obatizanso awo anaikidwa madzi pamutu kapena anabatizidwa akali ana. Cifukwa ndi ici ma Baptist amakhulupirira kuti amene okha anakhulupiliradi ndikusiya zocimwa zao anayenera kubatizidwa. Ma Baptist amakhulupilira kuti njira yeni - yeni ya Baibulo yobatiza ndiyo yolowa m'madzi (Kuikidwa m'madzi).

## MA BAPTIST AMAKHULUPILIRA CIANI?

Citenga miyezi kuphunzira ndikucita zimene ma Baptist amacita. Tidzangolankhula zocepa zokha zimene ma Baptist amakhulupilira ndikucita.



PHUNZILO 13

## KUBWERANSO KWA YESU KRISTU

BUKU LA PHUNZILO: 2 Petro 3:1-4.

VERSI LA PAMTIMA: "Taonani, adza ndi mitambo; ndipo diso liri lonse lidzampenya Iye." Cibuumbulutso 1:7a.

Muli zinenero zambiri m'cipangano cakale zokambapa kubweranso kwa Ambuye. Nthawi zina zinenerozi zitiphunzitsa Kuti Mesia amene abwela adzakhala oweruza wamphamvu, mfumu yaikulu, odziwika ndi olemekezeka ndi anthu onse. Zinenero zina zitiuza Kuti adzakanidwa, ndi kunyozedwa ndi Ku phedwa. Ena akhoza kudabwa cifukwaninji zinenero zisiyana pokamba za munthu m'modzi. Tiyenera kuzindikila za ici: cinali cifuniro ca Mulungu Kuti Yesu abwele kudziko la pansi kawiri.

Nthawi yoyamba Yesu anabwela, Anabwera monga mpulumutsi kudzasauka ndikudzafa cifukwa ca macimo a dziko la pansi. Atacita ici, anakwaniritsa zinenero zimene zinakamba za nchito yace yakupulumutsa. Tiphunzila mbuku Lopatulika kuti Ambuye adzabweranso. Pakubweranso kwace, adzakwaniritsa zinenero zokamba za mphamvu yace ndi ulemelero. Muphunziro ili, tidzaphunzila malemba ena amene atiphunzitsa za kubweranso kwa Ambuye.

## CITSIMIKIZIRO CAKUBWERANSO KWACE

Phunziro la mau a lero, Petro auza a Kristu Kuti anthu aucimo adzaseka cifukwa cakumva ciphunzitso pazakubweranso kwa Yesu. Awakumbutsa Kuti cinalinso cimodzimodzi m'masiku a Nowa. Mulungu ananena Kuti dziko la pansi lidzadzala ndi madzi. Koma sanakhulupirila mau a Mulungu, ndipo anafa pakudzala madzi m'dziko. Kusakhulupirila kwao sikunasintha kuona kwa Mau a Mulungu.

Cimodzimodzi leronso. Pali ena amene anena, "Yesu ali Kuti? Inu aKristu mwakhala muli kumuyembekeza kwa nthawi yaitali. Bwanji Sabwera?" Ali kuseweletsa lonjezano limodzi la malonjezano a Mau a Mulungu. Petro

## YANKHO KU MABVUTO AMIPINGO YATSOPANO

Ciri cinthu ca mabvuto pamene anthu amanena, "Ici ndico ndiganiza." Kuli bwino kunena kuti, "Ici ndico Mulungu anena." Mpingo yatsopano imene inayambidwa ndi Paulo ndi a Kristu ena, inayamba kukhala ndi mabvuto. Mwina anaiwala zinthu zina anaphunzitsidwa. Mwina a phunzitsi onama anadza mu mpingo ndikusintha coona cimene anaphunzila. Mulungu sanafuna anthu ace kukhala osokonezeka mwa aphunzitsi onama osadziwa coona. Cifukwa cace, pamene mabvuto anayamba m'mipingo, Mzimu Woyera unaphunzitsa ophunzira cifuniro ca Mulungu pa mabvutowo. Ndipo analemba makatata ku mipingo kuwauza m'mene Mulungu afunila kuti akhale okhulupirila ndiponso m'mene afunila Kuti akhalire. Tipeza makalata awa mbali yotsiriza ya Cipangano ca Tsopano, mu Aroma ndi Cibvumbulutso.

Mabvuto ambili amene tiona lero wayekha wayekha Kapena m'mipingo ndi mabvuto amene aKristu anali kuona kale. M'mau a Mulungu tikhoza kuphunzira cifuniro ca Mulungu pa mabvuto awa Werengani 2 Timoteo 3:15-17. Mpingo umene uwerenga ndikumvela mau a Mulungu ndi mpingo wolimba. Udzabweletsa osocera ambili kwa Yesu.

-ooOoo-



1. UMBUYE WA YESU KRISTU.

Ma Baptist amakhulupilira kuti Yesu Kristu ndi Mwana wa Mulungu wa yekha ndi kuti Iye ndi Ambuye wakumwamba ndi wapansi pano. Tiyenera kumvera Iye cifukwa Iye ndi Ambuye ndi wolamulira miyoyo yathu.

2. ULAMULIRO WENI-WENI NDIKUKWANILITSIDWA KWA CIPANGANO CATSOPANO MU ZINTHU ZA CIKHULUPILIRO NDIKUCITA KWACE.

Ici cithanthanza kuti timatenga ziphunzitso zathu kucokera mu Baibulo. Timakhulupilira kuti Mulungu anadzionetsa Yekha mwa Kristu, monga zinalembedwa Baibulo, ndipo Mulungu kwa ife.

3. KULEMEKEZEKA NDIKUTHA KWA MOYO MU ZINTHU ZACIPEMBEDZO.

Ma Baptist akhulupilira kuti kuli mtetezi m'modzi yekha pakati pa munthu ndi Mulungu, Yesu Kristu Ambuye wathu. Sitifunanso ansembe kapena anthu ena okhala otitezera ife kwa Mulungu. Munthu ali yense akhoza kupemphera kwa Mulungu kupyolera mwa Kristu ndipo akhoza kumveka ndi Mulungu.

4. KUFUNIKA KWAKUBADWANSO KWA TSOPANO.

Ma Baptist akhulupilira kuti munthu ali yense amene afuna kulowa kumwamba AYENERA kubadwanso kwatsopano mu mzimu. Kubadwa kwatsopano uku kutheka ndicisomo ca Mulungu mukukhulupilira osati ndikanthu kali konse kamene tiyenera kucita ife eni kuti tilandile kubadwa kwatsopano uku.

5. KUDZILAMULIRA KWA CHURCH YAPAMUDZI.

Munthu ali yense wa church ya Baptist ali ndi kusankha kamodzi, Wosowa ali ndikusankha kamodzi, ngakhare mbusa ali ndikusankha kamodzi.

6. UFULU WACIPEMBEDZO NDI KUKHARA MOSIYANA PAKATI PA CHURCH NDI ULAMULIRO WA DZIKO.

Ma Baptist ali omveka cifukwa cakulimbika kwao kunenetsa za ufulu kusiyana ndi ulamuliro wa dziko zinthu za kziko ndi za olamulira dziko zinthu za mzimu ndi za church. Cotero, tikhulupilira kuti Baibulo iphunzitsa kuti anthu ayenera kukhala anthu abwino mdziko lao.

7. LAMULO LA UBATIZO NDI NGONERO WA AMBUYE.

Ma Baptist amakhulupilira kuti kuli malamulo awiri okha mu Cipangano Catsopano, Ubatizo ndi Ngonero wa Ambuye Lamulo loyamba inapelekedwa pamene Kristu anayamba ulaliki wace, lamulo laciwiri inapelekedwa kutha kwa ulaliki wa Kristu. Malamulo onse ndizithunzi ndipo sizipulumutsa kapena kuthandiza kuti munthu apulumuke.

-ooOoo-





Mpingo unali ndi uthenga wa bwino. Uthenga uwu unali cipulumutso ndi moyo wosatha mwa kulapa mcikhulupirilo mwa Yesu. Mpingo unalamulidwa kukafalitsa uthenga uwu. Mpingo unapatsidwa mphamvu kuti ukwaniritse nchitoyi. Koma monga tiwerenga mitu yoyamba ya Macitidwe, tipeza Kuti mpingo sunayesa kuphunzitsa kubwalo kwace kwa Yerusalemu. Anali okondwera ndi nchito yabwino anaigwira m'menemo. Mwina anaiwala cimene Yesu anawalamulira.

Kuphedwa kwakukuru kwa mpingo kunayambidwa ndi a tsogoleri a Yuda. AKristu anathawira ku malo ena kupulumutsa miyoyo yao. Ndipo, m'malo ao atsopano anayamba kupemphera Ambuye ndi kuuza ena za Iye. Pameno anthu anamva za uthenga wa cipulumutso, analapa ndipo anapulumutsidwa. Ncosakondweretsa poona kuti aKristu sana tumizidwa kumalo ena ndi mpingo wa mu Yerusalemu. Anathamangitsidwa ndi iwo amene anawada ndikufuna kuwapha. Ciri cokondweretsa poona kuti, pamene anapiti'Kitsidwa m'malo osiyana-siyana, anali okhulupirika kumpembedza Mulungu, wao. Poyenda m'malo atsopano, tikhoza kupeza kuti Mpingo wa Baptist kulibe kumalowo. Tikhoza kukhala ngati ophunzila akalewo poyamba kuuza anthu za Yesu. Mnjira iyi mipingo idzayamba, Monga inayamba mipingo yakale.

Monga tiwerenga mu Macitidwe 13, tiphunzira kuti Mau a Mulungu anayamba kufalitsidwa. Nthawi iyi sicinali cifukwa ca kuphedwa. Atsogoleri ena a mpingo ku Antiokeya anali kusala kudya ndi kupemphera. Mzimu Woyera unati kwa iwo, "Mundipatulire ine Barnaba ndi Saulo ku nchito imene ndinawaitanirako." Macitidwe 13:2. Mpingo unatuma Paulo ndi Barnaba pa ulendo woyamba wokalalikira Mau a Mulungu. Popitiriza kuwerenga Macitidwe 13 tipeza Kuti mizimu yambili inapulumutsidwa ndi mipingo yatsopano inayamba. Uku kunali kufuna Mau a Mulungu kufika kutali. Mipingo yathu ikhoza kucita cimodzimodzi. Mwakupemphera ndikufuna kutsogozedwa ndi Mulungu, Mzimu Woyera udzawasonyeza malo ena amene afuna kumva mau a Mulungu. Ndipoakhoza kupeza njira Kuti uthenga wa Yesu ulalikidwe simalo aja.

Tiyeni tiganizire za mpingo umene Yesu anapatsa nchito iyi. Coyamba, tiyenera kumvetsetsa: ndi mpingo wa Yesu. Unamangidwa ndi Iye. Unamangidwa pa Iye. Siuli wa munthu ali yense. Tiwerenga mu Mateyu 16 m'mene Petro anabvomelezera cikhulupirilo mwa Yesu Kristu, Mwana wa Mulungu Wamoyo. Yesu ananena kuti adzamanga m'pingo wace. Mpingo sunamangidwa mwa Petro. Ici cikambidwa bwino mu buku la 1 Akorinto 3:11. "Pakuti palibe munthu akhoza kuika maziko ena, koma amene aikidwako, ndiwo Yesu Kristu." Ngakhale Paulo anayamba nchito ku Korinto ndi ena amene analalikilako, Paulo anafuna anthu kudziwa kuti Yesu yekha anali ciyambi ca Mpingo. Unamangidwa mwa Iye. Mpingo uli wonse umene uli woona mwa cifuniro ca Mulungu uyenera kukhala womangidwa mwa Yesu Kristu pokhulupirila Iye.

## MPINGO UNAPATSIDWA MPHAMVU NDI YESU

Yesu atafa ndikuuka kwa akufa, anakomana ndi a-Kuphunzila ace nthawi zambili. Asanakwele ku mwamba, Yesu anawaitana onse kubwela pamodzi. Anawauza kupita kudziko lonse ndi kupanga ophunzila ena, kuwabatiza, ndi kuwaphunzitsa. Mateyu 28:19,20. Iyi inali nchito yaikulu kucitidwa ndi anthu ocepa. Yesu anadziwa ici, koma sanawauza kucita ici ndi mphamvu zao zokha ai. Ambuye wao anati Kwa iwo monga tipeza mu versi lokumbuka la lero.

Mu mutu wa ciwiri wa Macitidwe tiwerenga za m'mene Mzimu Woyera unafikira ndikupatsa mpingo mphamvu. Tsopano anali nayo mphamvu imene analibe ndi kale lonse. Tiyeni titenge citsanzo ca Petro. Petro anaonetsa mantha pakuweruzidwa kwa Yesu. Anakana kuti salikumudziwa Yesu. Patapita masiku makumi anai, ndipo atalandila Mzimu Woyera, Petro anaimilira ndikulalikila opanda mantha kwa khamu lalikulu la anthu. Ena a awa analinkulalikila ndiwo aja amene anapha Yesu. Komabe, Petro sanawaopanso ai. Tsikulo anthu zikwi zitatu anapulumutsidwa. Tsopano pokhala nao Mzimu Woyera wakuwapatsa mphamvu, Petro ndi anzace anali okonzeka kutumikira Ambuye.



PHUNZILO 1

## BUKU LOPATULIKA LATHU - NDILO CIANI?

BUKU LA PHUNZILO: 2 Petro 1:12-21.

VERSI LA PAMTIMA: "Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa paciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca mcilungamo." 2 Timoko 3:16.

Buku lopatulika ndilo ciani? Buku Lopatulika ndilo buku lodziwika koposa mdziko lonse la pansi. Ambili a ife tili nalo bukuli ndipo mwina tinamuona munthu ali kuwelenga buku Lopatulika. Kodi tiri kudziwa Cipangano ndico ciani? Mumiyezi italu ili kubwela tidzakhala tili kuphunzila za Cipangano. Muphunzilo ili tidzaphunzila m'mene Buku Lopatulika linale - mbedwela, ndi m'mene analilemba. Tidzaphunzilanso cifukwa ninji linalembedwa. Ici cidza tithandiza kuona cimene Buku Lopatulika liri.

## CIPANGANO - MAU AMULUNGU

"Bukulopatulika" liri losiyana ndi mabuku ena adziko la pansi. Ndi buku limodzi lokha lokamba za Mau a Mulungu. Paulo analemba kuti "Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu." 2 Timoteo 3:16. Lemba ndilo dzina lina la Buku Lopatulika. Paulo anati Mulungu ndiye analemba Buku Lopatulika. Pokhala Mulungu mlembi wa Buku Lopatulika, lirinso buku loposa padziko lapansi.

Buku Lopatulika liri ndi uthenga wa Mulungu kwa anthu onse. Bukuli litiuza m'mene tingapulumukire ku macimo athu. Licitira umboni wa Yesu, potifera ife. Paulo analemba kuti, "Pakuti ndinapereka kwa inu poyamba, cimenenso ndinalandila, kuti Kristu anafera zoipa zathu, monga mwa malembo. 1 Akorinto 15:3. Buku Lopatulika litiuza m'mene tingakha lire ndi cimwemwe m'dziko lino ndi m'mene tingakonzekere pa mbuyo pa imfa. Buku Lopatulika ndi buku la mphamvu.

## CIPANGANO - M'MENE CINAPANGIDWILA

"Cipangano" ndi dzina lopatsidwa kwa buku lochedwa "Uthenga wabwino." Nthawi zina Cipangano cichedwa "Buku Lopatulika." Popeza Mulungu ndiye mlembi wa bukuli. Dzina la Kunena "Cipangano" litanthauza buku. Monga taona, liri buku loposa mabuku ena onse adziko lapansi. Kodi linalembedwa bwanji?

Cipangano ciri ndi mabuku ang'ono ambili amene tiwacha "mabuku a Mcipangano." Tiona kuti mabuku awa ali ndi maina osiyanasiyana - Genesis, Mateyu, Luka, Yohane, ndi ena ambili, Muli ma buku 66 m Cipangano. Kale mabuku 66 awa anaikidwa pamodzi kupanga buku lalikulu limodzi lochedwa Cipangano.

Mabuku ang'onowa ndi ogawidwa m'madela awili. Dela loyamba liri ndi mabuku 39 ndipo lichedwa Cipangano cakale. Linalembedwa Yesu asanabadwe. Dela la ciwili liri ndi mabuku 27 ndipo lichedwa Cipangano ca Tsopano. Linalembedwa Yesu atakhala kale pa dziko la pansi.

Cipangano cinalembedwa zaka zambili zapita, koma uthenga wace sukalamba iai. Bukuli liri ndi uthenga wa Mulungu kwa anthu onse kunthawi zonse.

## CIPANGANO - M'MENE CINALEMBEDWELA

Mulungu analemba Buku Lopatulika. Kodi Mulungu analilemba bwanji Buku Lopatulika? Mulungu anafuna anthu kuti aulembe uthenga wace wa kwa anthu onse. Nthawi zina anthu amasokonezeka ndi ici, popeza timati Cipangano ndiwo mau a Mulungu ndiponso timati anthu monga Mose, Davide, Mateyu ndi ena analemba bukuli. Mulungu anafuna anthu ena kusindikiza uthenga wace. Umu ndi m'mene Petro ana fotokozela aKristu ena kale kale. "Pakuti kale lonse cinenero sicinadza ndi cifuniro camunthu; koma anthu a Mulungu, ogwidwa ndi Mzimu Woyera, analankhula." 2 Petro 1:21. Mau a kulu mu versi ili ndi awa ".........sicinadza - ndi cifuniro camunthu.......koma anthu a Mulungu - Ogwidwa ndi Mzimu Woyera." Ici cititsimikizila kuti Cipangano sicinalelembedwa ndi anthu popeza anthu anafuna kucilemba. Koma



PHUNZILO 12

## KUYAMBA KWA MIPINGO YOYAMBA

BUKU LA PHUNZILO: Mateyu 16:13-20; Macitidwe 2:1-47.

<u>VERSI LA PAMTIMA</u>: "Komatu mudzalandila mphamvu, Mzimu Woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'-Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'samariya, ndi kufikiro malekezero ace a dziko." Macitidwe 1:8.

Sabata latha tinaphunzila za moyo, ifa, ndi kuukanso kwa Ambuye Mpulumutsi, Yesu Kristu. Pamene Yesu anali pa dziko la pansi, Anacita zodabwitsa zambili. Coposa cimene Yesu anacita akali pano padziko la pansi ndico kupereka cipulumutso kwa dziko lapansi losocela. Atiuza kuti ndico cifukwa cace anabwela padziko la pansi. "Pakuti mwana wa munthu anadza kufunafuna ndi kupulumutsa cotaikaco." Luka 19:10.

Tiyenera kukumbuka coonadi cina. Yesu akali pano pa dziko, sanayenda kwambili monga tikhoza kuyenda lero. M'masiku aja kunalibe ndege, masitima, magalimoto ndi sitima zoyenda m'madzi. Yesu anakhala ndipo anafa m'dziko laling'ono. Malo okwanila pafupi 40 mailosi kum'mawa ndi kumadzulo ndiponso 125 mailosi kumpoto ndi ku m'mwela akhoza kukwanila ulendo wace. Mtunda wa Kumpoto ndi ku m'mwela ucepa ndi mtunda wakucoka ku Broken Hill kunka ku Kitwe. Kodi cifuniro ca Yesu cinali cotani pofuna kupulumutsa dziko lonse la pansi pamene ciphunzitso cace cinali m'dela laling'ono lotere ndiponso kwa anthu ocepa?

## MPINGO UNAKHAZIKITSIDWA NDI YESU

Umu ndim'mene Yesu anakonzela kuti dziko lonse lipulumutsidwe. Anadzipereka ku imfa ya pamtanda cifukwa ca macimo a dziko lonse. Ndipo anauza mpingo wace kukauza anthu onse zambiri yabwinoyi. Ili mbili ya bwino di kudziwa kuti kupyolera m'kulapa ndi kukhulupirira mwa Yesu munthu akhoza kulandila cipulumutso, ndicikhululukiro ca macimo ndi moyo wosatha.

nasiyana kwa ophunzila ace ndi anthu ena. Nthawi ina anaonekera kwa anthu oposa mazana asanu. 1 Akorinto 15:6. Patapita masiku makumi anai atauka kwa akufa, Kristu anakwera kumwamba. Asanakwele kumwamba anati kwa ophunzila ace: "Mukani kudziko lonse la pansi, lalikilani uthenga wabwino kwa olengedwa onse." Marko 16:15. Onaninso Mateyu 28:18-20.

Pali zinthu zina zimene tiyenela kuphunzila mu phunzilo ili:

1. Yesu ndiye Mwana wa Mulungu.

2. Anabadwa ndikukhala monga ife tikhala lero. Anayesedwa, koma anapambana mayesero. Ndipo adzapatsa ana ace mphamvu yaku pambana mayesero lero.

3. Yesu anapereka moyo wace pamtanda kuti inu ndi ine tikhale ndi moyo wosatha.

4. Tikhoza kukhala ndi moyo wosatha pakulapa macimo athu ndikulandila Kristu kukhala Mpulumutsi ndi Ambuye.

5. Kristu ayembekeza ife kuuza ena za Iye.

Pakati pasabata phunzilani mabuku oyamba anai a Cipangano ca Tsopano: Mateyu, Marko, Luka, Yohane.

(Mwakupitiriza kuphunzila kwanu werengani mabuku awa: Luka 1:5-38; Luka 2:1-20; Luka 2:41-52; Mateyu 3:1-4; Mateyu 3:13-17; Yohane 11:32-44; Mateyu 28.)

-ooOoo-



Cipangano cinale - mbedwa ndi anthu ogwidwa ndi mzimu Wace. Mulungu sanagwetsa Cipangano padziko colembedwa kale, koma anagwilitsa anthu nchito kulemba uthenga wa Bukuli. Cifukwa cace, pamene tiphunzila za uthenga wa Cipangano, tiphunzila uthenga wa Mulungu.

## CIPANGANO - CIFUKWANINJI CINALEMBEDWA

Mu versi lathu la pamtima, Paulo akuti Cipangano ndi cabwino m'cipembedzo ndi mcilangizo ca m'cilungamo." Ici citanthauza kuti Cipangano citiuza makhalidwa kutiuza nji'ra ya cipulumutso. Cipangano cimatiuza za cikondi ca Mulungu. Tiuzidwa m'mene Yesu anatifera pamtanda ndi m'mene tingadziwire Mulungu kupyolera mwa Yesu. "Pakuti Mulungu anakonda dziko la pansi kotero, kuti anapatsa mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wokhulupirila Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha." (Yohane 3:16). Cipangano citiuza njira yakukhala mkristu Koma citiuzanso m'mene tingakhalire ngati a Kristu. Monga Paulo anena, "Lemba liri lonse adaliuzi la Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonsero, cilangizo ca mcilungamo: Kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kucita nchito ili yonse yabwino." 2 Timoteo 3:16;17.

Potsiliza tinganene kuti pali zifukwa ziwili cipangano cinalembedwela. Coyamba, Mulungu anapatsa Cipangano, kuti osocera osapulumutsidwa akadziwe njira ya cipulumutso. Paulo anati za Malemba "Okhoza kukupatsa nzeru kufikila cipulumutso, mwa cikhulupirilo ca mwa Kristu Yesu." 2 Timoteo 3:15. Tiyenela kukumbukila kuti Yesu apulumutsa ife ndi Cipangano citiphunzitsa za Yesu. Caciwili, Mulungu anapatsa cipangano kwa anthu kuti apulumutsidwa akadziwe njira ya cikristu.

## CIPANGANO - CINAPATSIDWA KWA YANI

Kodi Mulungu anapatsa kwayani Buku Lopatulika? Yankho la funsoli lipezedwa m'cikondi ca Mulungu. Kodi Mulungu akonda yani? Mulungu akonda anthu onse. "Pakuti Mulungu anakonda dziko la pansi kotero." Cifukwa cace Mulungu anatuma athenga wace kwa anthu onse. Buku Lopatulika si buku la dziko limodzi kapena ntundu umodzi wa

anthu ai. Cipangano ca Kale cinalembedwa m Cihebri poyamba ndipo Cipangano ca Tsopano cinalembedwa m ci giriki. Koma cinathanthauzidwa mzilankhulidwe zina zambili. Cinali cifuniro ca Ambuye Kuti Mau a Mulungu alalikidwe kwa anthu onse. Asanakwele kunka kumwamba analamulira ophunzila ace Kuti: "Cifukwa cace, mukani, phunzitsani anthu amitundu yonse, ndikuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndikuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndili pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimaliziro ca nthawi ya pansi pano." Mateyu 28:19,20.

Ndiponso Buku Lopatulika lili la anthu onse kunthawi zonse. Buku Lopatulika silidzakhala la kale. Buku Lopatulika ndiwo mau a Mulungu ndi uthenga wace kwa anthu onse. Yesu anati, "Thambo ndi dziko la pansi zidzacoka, koma Mau anga sadzacoka ai." Mateyu 24:35.

Petro anali, "Koma Mau a Mulungu akhala cikhalire." 1 Petro 1:25. "Udzu unyala, duwa lifota, koma Mau a Mulungu wathu adzakhala nthawi zacikhalire." Yesaya 40:8.

<u>KUTSILIZA</u>: Popeza tili ndi Cipangano, tili ndinchito yaikulu. Yesu anati, "Iye amene akaniza Ine, ndi kusalandira mau anga, ali naye womweruza iye; mau amene ndalankhula, iwowa adzamweruza tsiku lomariza." Yohane 12:48. Sitikhoza kutsutsa uthenga wa Buku Lopatulika opanda kuweruzidwa tsiku lina. Tiyenera Kuganizila ciani za Cipangano, Coyamba, Tiyenera Kuonga Mulungu Kuti Ali ndi Mau ace otiuza njira ya cipulumutso, ndi moyo umene Iye afuna ife kukhalamo. Ndipo tiyenera kuphunzila Cipangano ndi kumvela mau ache.

-ooOoo-



## ULALIKI WACE

Tiyenera kukumbukira kuti Yesu sanacimwa. Anakhala padziko monga inu ndi ine tikhala. Anayesedwa kucita coipa monga inu ndi ine timayesedwa. Koma sanacimwa, ngakhale kamodzi. Tiyeni tiwerenge mau awa mu Ahebri 4:15b: "Koma wayesedwa m'zonse monga momwe ife, koma wopanda ucimo."

Yesu anaonetsa zodabwitsa zambili akali pano padziko. Anacilitsa anthu ambili amene anali odwala. Osapenya anaona. Anautsa akufa kwa akufa. Yesu anali ndi mphamvu yakulamulira mphepo ndi mafunde a mnyanja. Makamu a anthu anamutsata. Anafuna Yesu kukhala mfumu yao yapano pansi. Koma sanafika pa dziko la pansi kukhazikitsa ufumu wa dziko lapansi. Anadza kukhala m'mitima ya anthu.

Panali anthu khumi ndi awili amene anali ndi Yesu nthawi yonse pa zaka zitatu za ulaliki wace pano pansi. Anthu awa anachedwa ophunzila. Yesu anawaphunzitsa za cikondi ca Mulungu pa anthu onse. Anali ndi Iye pamene anali kucita zodabwitsa. Anaona mphamvu ya Mulungu mwa Yesu. Pa zaka izi, Yesu anayesa kuphunzitsa ophunzila ace cifukwa cace anabwela pa dziko. Versi lathu lokumbuka litiuza bwino bwino cifukwa cimene Yesu anabwerera padziko la pansi. Mulungu akonda anthu onse. Anatuma Mwana wace, Yesu Kristu, kudzafera macimo athu.

## IMFA YACE

Yesu anapita ku Yerusalemu mumasiku otsiliza autumiki wace padziko la pansi. Komweko anapelekedwa ndi m'modzi wa ophunzila ace. Adani ace anamutenga Iye. Anabwera naye Yesu pamaso pa oweruza Kuti aweruzidwe. Potsiliza, anapacikidwa pamtanda. Pamtanda, Yesu amene sanadziwa cimo, anapeleka moyo wace kuti tikhale nao moyo wosatha. Atafa, anaikidwa kumanda.

## KUUKANSO KWACE

Patsiku lacitatu, Yesu anauka kwa akufa. Codabwitsa: Kristu anagonjetsa imfa. Atauka, anaonekera nthawi zosiya-

ndi kubwela kwa Yesu, Mpulumutsi wathu. Mariya ndi Yosefe analikufuna kukwatilana. Tsiku lina m'ngelo wa Mulungu anafika kwa Mariya. "Ndipo m'ngelo anati kwa iye, Usaope, Mariya; pakuti wapeza cisomo ndi Mulungu. Ndipo taona, udzakhala ndi pakati, nudzabala mwana wamwamuna, nudzamucha dzina lace Yesu." Luka 1:30,31. Mariya anati, "Ici cidzacitika bwanji, popeza ine sindidziwa mwamuna." Luka 1:34b. M'ngelo anayankha: "Mzimu Woyera adzafika pa iwe, ndi mphamvu ya Wamkulukulu idzakuphimba iwe cifukwa cacenso Coyeraco cikadzabadwa, cidzachedwa Mwana wa Mulungu." Luka 1:35. Yosefe anabvutika mumtima mwace. Koma m'ngelo anamutsimikizila kuti zonse zinali bwino. (Onani Mateyu 1:19-21).

## KUBADWA KWACE

Nthawi itakwanila, Yesu anabadwa mu Betelehemu. Sitidziwa kwambili za unyamata wace wa Yesu. Luka atiuza nthawi pamene Yesu anali ndi zaka khumi ndiziwili. Anapita ndi Mariya ndi Yosefe ku Yerusalemu. Akali komweko, Analankhula ndi akulu a mpingo a thawi ija, Anadabwa cifukwa ca nzelu zace. Luka atiuza ici pa zaka zoyamba za Yesu. M'moyo wace "Ndipo Yesu anakulabe m'nzeru ndi mumsinkhu, ndi m'cisomo ca pa Mulungu ndi ca pa anthu." Luka 2:52.

## UBATIZO WACE

Pamene Yesu anali pafupi zaka makumi atatu, Mulungu anatuma Yohane Mbatizi kukakonza anthu kuti alandire Yesu. Yohane analalikila ndikuuza anthu kuti alape. Iwo amene analapa anabatizidwa monga cizindikiro cakulapa ndikukonzekera kulandila Yesu Kristu pamene atabwera. Pamene Yesu anali okonzeka kuyamba ulaliki wace, Anapita kwa Yohane nabatizidwa mumtsinje wa Yordano. Ubatizo sunapulumutsa Yesu. Cinakhala cidziwitso mu Ufumu wa Mulungu. Anacita ici cifukwa cakumvera Mulungu. Comweconso ubatizo sutipulumutsa ife. Citisonyeza ife kuti tili otsatira a Yesu ndiponso monga ngati omvera lamulo la Yesu. Ndipo cionetsanso dziko lapansi cimene cacitika m'moyo wathu, pamene tibvuomereza Kristu kukhala Mpulumutsi.



PHUNZILO 2

## CIPANGANO - M'MENE TIDZIWIRA KUTI NDI COONA

BUKU LA PHUNZILO: Masalmo 19:7-11.

VERSI LA PAMTIMA: "....Ndi cilamulo canu ndico coonadi" Masalmo 119:142b.

## CIPANGANO - UTHENGA WOONA WACIPULUMUTSO

Pa dziko lonse la pansi pali khumbo la kufunitsitsa nzelu. Ambili ali kupita kusukulu kukaphunzila. Muno m' dziko lathu la Zambia, tiona kuti muli njala yaikulu ya maphunzilo. Cifukwa cace anthu alikufunila kuphunzila masiku ano ndico kuti afuna kupeza coona ca m'moyo uno. Ciri ca bwino kuti anthu aphunzile kuwerenga ndi kulemba. Mkutero akhoza kudzipezela okha cabwino m'moyo wao. Mpingo wa Baptist, umene umalalikila za Cipangano, umafuna anthu kufuna coonadi iwo okha. Paulo analemba mu 2 Timoteo 2:15, "Ucite cangu kudzionetsela kwa Mulungu wobvuomerezeka, wa nchito wopanda cifukwa cakucita manyazi, wolunjika nao bwino mau a coonadi." Ife amene tiri a Baptist tili osaopa anthu kutifunsa za cikhulupirilo cathu cifukwa ciri cocokera m Cipangano.

Pali maphunzitso ambiri pa dziko la pansi nthawi ino amene aitana anthu kuwatsata. Maphunzitso ambili awa amati ali naco coonadi. Nanga coonadi ndi ciani? Ife a Baptist tili ndi uthenga woona wa Mulungu kwa anthu onse. M'maphunzitso onse a dziko la pansi, ife timamva mau a Mulungu Kucokela m'Buku Lopatulika. Timakhulupirila Kuti Buku Lopatulika ndilo lokha muli uthenga wa Mulungu wa kwa anthu onse pa za cipulumutso. Tiyeni tiganizile za ciphunzitso cathu ngati ciri nao mau ogwirizana naco. Pano pali zifukwa zimene zitipatsa ife cikhulupirilo kuti Buku Lopatulika liri loona.

## CIPANGANO - M'MENE TIKHULUPIRIRA KUTI NDI COONA

1. Amene analemba Cipangano anati anatsogozedwa ndi

Mulungu. Anthu amene analemba Cipangano anati analikulankhulira Mulungu. "Imvani, miyamba inu, chera Makutu, iwe dziko la pansi, cifukwa Yehova wanena." Yesaya 1:2. "Ndipo anadza kwa ine Mau a Yehova kuti" Yeremiya 1:4. "Pakuti ndikudziwitsani inu, abale, za Uthenga Wabwinowo wolalikidwa ndi ine, kuti suli monga mwa anthu. Pakutitu sindinaulandila kwa munthu, kapena sindinauphunzila, komatu unadza mwa bvumbulutso la Yesu Kristu." Agalatiya 1:11,12. Anthu amene analemba Cipangano anakhulupirila Kuti unali uthenga woona wa Mulungu. "Mwa Iyeyo inunso, mutamva mau a coonadi, Uthenga Wabwino wacipulumutso canu." Aefeso 1:13. "Mwacifuniro cace mwini anatibala ife ndi mau acoonadi." Yakobo 1:18. "......Ndicilamulo canu ndico coonadi" Masalmo 119:142b.

Muli ma versi ena ambili m'Cipangano amene aonetsa kuti iwo amene analemba Cipangano analemba uthenga wa Mulungu. Popeza anthu awa analemba monga Mulungu anawatsogolera, uli uthenga wa Mulungu ndipo tidziwa Kuti "Mciyembekezo ca Moyo wosatha, umene Mulungu, wosanamayo, analonjeza zisanayambe nthawi zosayamba." Tito 1:2.

2. Kugwirizana Kwa Cipangano Kuonetsa Kuti mau ace ali oona.

Cipangano cinalembe dwa ndi anthu amuna ambili ku zaka za nthawi yakale. Pali nthawi yokwanira zaka 1600 pamene analemba mabuku oyamba ndi otsiliza a Cipangano. Ndiponso, Cipangano cinalembedwa m'malo osiyanasiyana. Madela ena analembedwela m'cipululu, madela ena ku Palestina, ku Roma ndi Ku Babuloni, ndi malo ena ambili. Mlembi aliyense analemba yekha. Koma pamene zolemba zao zinasonkhanitsidwa ndikutsogoleredwa ndi Mzimu Woyera, anapanga buku limodzi ndi uthenga umodzi. Ici cionetsa Kuti Mulungu anatsogolera olemba polemba uthenga wace.

3. Za mkati mwa Cipangano zitsimikiza kuti ndi coonadi.

M'cipangano muli coonadi ndi malonjezo amene sanakalingirilidwa ndi muthu yekha. Coyamba, muli coonadi m Cipangano cinene munthu sanadziwa opanda



PHUNZILO 11

## KUBWELA KWA MPULUMUTSI

BUKU LA PHUNZILO: Mateyu 1:18-25; Mateyu 28:1-20; Yohane 19:28-30; Yohane 19:38-42.

<u>VERSI LA PAMTIMA</u>: "Pakuti Mulungu anakonda dziko la pansi kotero, Kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirila Iye asatayike, Koma akhale nao moyo wosatha." Yohane 3:16.

### UNENERI

Mu phunzilo tinaphunzila masabata awili apitao, tinaphunzila za lonjezo limene Mulungu anapatsa kwa Adamu ndi Hava. (Werengani Genesis 3:15). Tinaphunzilanso kuti anapatsanso lonjezo lomwelo kwa Abrahamu mu buku la Genesis 12:3. Mu buku lonse la Cipangano ca Kale, tipeza mau a cidziwitso ca Kubwela kwa mpulumutsi, Yesu Kristu.

Mu Yesaya 7:14 tipeza mau awa onenera: "Cifukwa cace Ambuye mwini yekha adzakupatsani inu cizindikiro: taonani namwali adzaima, nadzabala mwana wa mwamuna, nadzamucha dzina lace Imanueli." Ndiponso Yesaya ana" lemba mau awa: "Pakuti kwa ife mwana wakhanda wabadwa, kwa ife mwana wamwamuna wapatsidwa, ndipo ulamuliro udzakhala paphewa lace, ndipo adzamucha dzina lace Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu wa Mphamvu, Atate wosatha, Kalonga wamtendere." Yesaya 9:6.

Cinanenedwa Kuti Betelehemu ndiwo malo obadwilamo Yesu. (Onani Mika 5:2). Mu Yesaya 53 mabvuto c Mpulumutsi wathu ananenedwa poyamba. Anapeza mabvuto awa kuti apulumutse inu ndi ine kumacimo athu. Muyenera kuwelenga mutu wonse wa bukuli kunyumba yanu.

### KUFALITSA

Zaka zambili zinapitapo pakati, pamene aneneri ananenera zakubadwa kwa Yesu ndi kubwela kwa Yesu,

kumacimo ao. Potsiliza Mulungu sanakondwela ndi njira zao ndipo analora Asuri kugonjetsa Aisrayeli. Ambili aiwo anakhala akapolo.

Yuda, ufumu wakumadzulo, unali ndi mafumu abwino ndi ena oipa. Pamene mafumu abwino anatsogolera anthu mnjira zabwino, Mulungu anawadalitsa Pamene anakana cifuniro ca Mulungu, Mulungu anawalanga. Macimo ao anakulabe, ndipo Mulungu analora kuti agonjetsedwe ndi kutengedwa ukapolonso.

Patapita zaka makumi a sanu ndi awili zaukapolo, Ayuda ena analoledwa kubweleranso ku Yerusalemu, Ndipo anamanganso mzinda ndi kacisi. Anaphunzila phunzilo limodzi bwino. Sanayendanso m'njira zaciwerewere.

ANENERI

Nthawi ndi nthawi Mulungu anatumiza aneneri kwa mafumu Aisrayeli ndi Yuda. Nthawi zina anawamvela aneneri koma nthawi zina sanawamvera. Anthu anamvela kwa anthu amene anaphunzitsa zimene iwo anafuna kumvera. Mneneri wotsiliza amene Mulungu anatumiza ndiye Malaki. Ananenera zaka zikwi zinai Yesu asanabwele.

Pano pali zinthu zimene tifunika kuphunzila za phunzilo ili:

1. Mulungu afuna kudalitsa anthu ace. Koma anthu ayenera kukhala m'njira imene Mulungu angawadalitsilemo.

2. Kukana uthenga wa Mulungu ndiko kukana Mulungu Mwini.

3. Pamene munthu akana kumvera Mau a Mulungu, Mulungu akhoza kusiya munthu uja mu ndima opanda uthenga uli wonse.

Kunyumba yanu, yambani kuphunzila maina otsala a Cipangano ca Kale. Munaphunzila mabuku asanu oyamba sabata latha.



Mulungu kucibvumbulutsa. Yesu anauza Petro, "Pakuti thupi ndi mwazi sizinakuululira ici, koma Atate wanga wa Kumwamba." Mateyu 16:17. Caciwiri, muli malonjezo ena mcipangano cakale amene tidziwa anakwaniritsidwa. Mwa citsanzo, malo ndi maonekedwe a malo m'mene Yesu anabadwila zinanenedwa zaka 700 pamene zikalibe kucitidwa. Tipeza mau awa kambili m cipangano catsopano. "Ndipo zonsezi zinakhala kuti cikacitidwe conenedwa ndi Ambuge mwa mneneri." Mateyu 1:22. Msunagoge wa ku Nazareti, Yesu anawerenga mu Yesaya 61 ndipo anatseka buku nati, "Lero lembo ili lakwanitsidwa m'makutu anu." Luka 4:21. Kodi anthu angadziwe bwanji zamtsogolo ndi kunenera? Pali yankho limodzi. Mulungu anawatsogolera. Cifukwa cace kukwaniritsidwa kwa malonjezo kuli koona.

4. Umboni wa Yesu uonetsa kuti cipangano cili coona.

Yesu anakhulupirila m Cipangano cakale. Yesu analankhula mau a m Cipangano cakale. Yesu analankhula mau a m cipangano cakale kuonetsa ophunzila ace kuti ndiye Mpulumutsi wolonjezedwayo. "Ndipo anayamba kwa Mose ndi kwa aneneri onse, nawathathauzila iwo m'malembo onse zinthu za Iye Yekha." Luka 24:27. Yesu anapatsanso ophunzila ace lonjezo limene tilipatsa kuzindikila kuti Cipangano Ca Tsopano cinalembedwa ndi utsogoleri wa Mzimu Woyera. "Koma Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, Iyeyo adzaphunzitsa inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu?" Yohane 14:26. Ici citanthauza m'mene alembi anasungila mau amene Yesu analankhula zaka zambiri pambuyo pace atazilankhula. Inde, Yesu anakhulupirila kuti Cipangano ciri coona.

5. Mphamvu ya Cipangano ionetsa Kuona kwace.

Pamene tikamba za mphamvuya Cipangano tinena zocita za Cipangano pa anthu. Ponse pamene Cipangano cabvomerezedwa, casintha miyoyo ya anthu. Cipangano cilankhula ku mitima yathu ndikutizindikiritsa kuti liri buku la Mulungu. Cipangano cimaomba belu mitima yathu pamene timva uthenga wace ndipo timadziwa kuti Mulungu alikutiitana. Pamene anthu amva uthenga wa Cipangano, amakhala

a cisoni cifukwa camacimo ao. Amalapa zoipa zao ndi kukhulupirila Yesu. Amayamba Kutsata Yesu ndi miyoyo yao yosinthika. Kusintha uku m'moyo wa munthu kudzasintha mudzi, boma, ulungu ndi dziko.

## CIPANGANO - KODI MUKHULUPIRILA NDI COONA?

Kodi mukhulupirila uthenga wa m'Cipangano. Anthu ambili anena Kuti akhuluprila Cipangano, koma satsata ziphunzitso zace. Ngati mukhulupirila kuti Cipangano ndiwo mau a Mulungu, mudzakhala mziphunzitso zace. Nanga atate wanu atakuuzani kuti mucite kanthu kena, ndipo ukana kucita. Akhoza Kukhala okwiya ndi inu. Mwina munganene kwa Iye. "Ndikukhulupirilani, atate. Ndikhulupirila zimene munena." Komabe simucita cimene atate wanu anakuuzani kuti mucite. Motero akhoza Kukhala okwiya ndi kukupatsani cilango, popeza simunaonetsa Kumkhulupirila pomumvela iye. Cimodzi modzinso ndi Mulungu. Tiyenela Kumvela zolembedwa m Cipangano, Kapena pali anthu ena ali kunena kuti "Ndifuna kudziwa ngati Cipangano ciri coona." Mulungu analonjeza aliyense Kuti adzamthandiza ngati afunadi Kutsata coona. Lonjezo lipezedwa mu Yohane 7:17, "Ngati munthu ali yense afuna Kucita cifuniro cace, adzazindikira za ciphunzitsoco, ngati cicokera kwa Mulungu, kapena ndi lankhula zocokera mwa ine ndekha." Yesani ziphunzitso za Cipangano. Mudzadziwa zili zoona.

-ooOoo-



kutsogolera anthu kunkhondo bwino. Sauli sanatsata cifuniro ca Mulungu. Anayamba kudzitama ndikukana njira ya Mulungu. Potsiliza Mulungu anafuma Samueli kuuza Sauli kuti Mulungu anamucokera. Ndipo kuti munthu wina adzakhala mfumu m'malo mwace. Sauli anadziwa kuti womulowela m'malo adzakhala Davide. Motero Sauli anayesa kupha Davide nthawi zambili. Mulungu, amene anasankha Davide, anamucinjiliza.

Potsiliza Sauli anaphedwa kunkhondo ndi Afilisti. Davide anaitanidwa kuweruza mtundu umodzi wa mitundu ina inafunsa Davide kukhala mfumu yaonso, Davide anakhala mfumu zaka makumi anai. Mu ufumu wa Davide, Aisrayeli anakhala mtundu wa mphamvu. Davide anali mfumu yopanda tsankhu ndipo anaopa Mulungu ndi kumvera Mulungu. M tundu unazindikira kuti Mulungu anali kudalitsa Aisrayeli cifukwa Aisrayeli analikupembedza Mulungu ndi kutumikira Mulungu woona ndi wa moyo.

Pamene Davide anakalamba anadzoza mwana wace Solomo, kuweruza m'malo mwace. Solomo anali munthu wanzelu. Mulungu anamudalitsa kweni-kweni. Mu ufumu wace mtundu unali wa chuma ndi wolemekezeka. Solomo anakwatira akazi ambili ndipo anamubweza pakutsata Mulungu bwino. Munali mu ufumu wa Solomo pamene nyumba yabwino ya Mulungu inamangidwa mu Yerusalemu.

## UFUMU WOGAWIKANA

Rehabiamu anakhala mfumu atafa Solomo, atate wace. Anthu anafunsa Rehabiamu kukhala wabwino koposa m'mene atate wace anali. Omuweluza mfumu anamuuza kuti abvomere. Koma anyamata anzace anamuuza kuti auze anthu kuti adzamugwirila nchito koposa. Rehabiamu anamvera mau a anyamata. Pamene anthu anamva ici, anamukana Rehabiamu kukhala mfumu yao. Ndipo ena anacoka nasankha Yerobiamu kukhala mfumu yao. Mitundu ina iwili, Yuda ndi Benjamini inatsatabe Rehabiamu.

Mafumu a mitundu ya kumwela (anazicha Israyeli) ndipo anali ocimwa. Anatsogolera mtundu m'macimo ambili. Anakana kumvela aneneri amene Mulungu anatuma kuwatsutsa

asasiyepo munthu wa anthu aja. Anadziwa kuti ngati anthu ace akhala pamodzi ndi kukwatilana ndi anthu oipa aja, iwonso posacedwa akadayamba kutsata coipa zao.

## NTHAWI YA OWERUZA

Ngakhale ana Aisrayeli analonjeza kumvela malamulo onse a Mulungu, analephela. Sanapha kapena kupitikitsa anthu aja onse eni dziko lija. Anayamba kukwatilana nao. Ndipo anayamba kumapembedza nao mafano. Kotero kuti kucimwa kwao kunakula kuti Mulungu sanawadalitsanso koma anaona kuti nkwabwino kuwalanga.

Njila imodzi imene Mulungu anawalanga nayo ndiyo yoti analola mitundu ina kuwagonjetsa ndi kuwaweruza. Panthawi iyi anali kusauka kwambili. Posaukatere anayamba kukumbukira m'mene Mulungu anali kuwadalitsila ndi m'mene anawapulumutsila ku adani ao poyambapaja. Analapa ndi kufunsa Mulungu kuwakhulukila ndikuwathandiza. Mulungu anali kumva kulira kwa anthu ace ndi kuwapatsa mtsogoleri wa mphamvu. Atsogoteri awa anachedwa (oweruza) zaka pafupi zikwi zitatu anthu awa anatsogoleredwa ndi oweruza osiyanasiyana. Inali nthawi imene anthu ocepa anali kudziwa Mau a Mulungu ndipo Kunalibe utsogoleri, wakuwalangiza njira za Mulungu. Makolo analephela kuphunzitsa ana ao ndi adzukulu ao za Mulungu. Timawerenga za nthawi iyo: "Yense anacita comkomera pamaso pace." Oweruza 21:25.

## UFUMU WOLUMIKIZIDWA

Oweruza woposa ndi wotsiriza anali Samueli. Tiwerenga za moyo wace ndi ciphunzitso cace mbuku loyamba la Samueli. Mu utsogoleri wa Samueli, mtundu unali wosatumikira Mulungu. Anthu sanafunanso oweruza kuwatsogolera. Anafuna mfumu monga mitundu ina. Samueli anapemphela kwa Mulungu pa cinthu ici. Mulungu anauza Samueli kuti anthu sanakana iye Samueli. Koma anakana Mulungu ndi ulamuliro wa Mulungu paiwo. Mulungu anauza Samueli kudzoza mfumu ya anthu awa.

Sauli anasankhidwa mfumu yoyamba. Anapatsidwa popeza anthu anafuna mfumu. Anali munthu wa mkulu okhoza



PHUNZILO 3

## CIPANGANO - UTHENGA WACE WAPAKATIKATI

BUKU LA PHUNZILO: Ahebri 1:1.

VERSI LA PAMTIMA: "Ndipo udzamucha dzina lace Yesu, pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ace kumacimo ao." Mateyu 1:21.

"Koma zalembedwa izi Kuti mukakhulupirile kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu, ndi Kuti pakukhulupirira mukhale nao moyo m'dzina lace." Yohane 20:31.

## CIPANGANO - WAMKULUKULU

Kodi mudziwa cifukwa colembedwela Cipangano? Mwina wina adzayankha, "Kudiuza makhalidwe." Ili siyankho lonse lokwanila. Linalembedwa kutiuza za munthu m'modzi - Yesu Kristu. Cipangano conse cili ndi mbiri ya Kudza Kwa Yesu pansi pano Kudzatifera, ndi ku tipulumutsa Ku mau cimo athu. Cipangano ca kale cilonjeza Kuti Yesu adzabweranso. Cipangano (Catsopano) Citiuza Kuti Yesu anadza. Citiuza phindu la Kudza Kwace Yohane analemba nchito ya buku lace. Kulemba kwace kwa mau a Mulungu kuli phunzilo la bwino la cipangano. "Koma (mau) awa alembedwa, kuti mukakhulupirire kuti Yesu ndiye Kristu." Yohane 20:31.

## CIPANGANO - CILONJEZA YESU MCIPANGANO CAKALE

Pamene Adamu anacimwa, anabweletsa cimo padziko. "Cifukwa cace, monga ucimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu m'modzi (Adamu) ndi imfa mwa ucimo; cotero imfa inafikila anthu onse, cifukwa kuti onse anacimwa. Aroma 5:12. Mulungu akadaononga anthu onse opanda cifundo nthawi ija. Koma anasankha kupatsa njira yacipulumutso kwa anthu. Cifukwa cace, analonjeza mpulumutsi, amene anakapulumutsa anthu ace kumacimo onse. Panali lonjezo la mpulumutsi pa mkwiyo wa Mulungu kwa njoka. "Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mKaziyo, ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalarila citende cace." Genesis 3:15.

M'mau awa muli lonjezo la iye amene adzagonjetsa satana.

Lonjezo iri linabwelezedwa nthawi zambili mzaka zimene zinatsatila. Yesaya ananeneratu za ici pamene analemba, "Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njila ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse." Yesaya 53:6. Anthu anayembekeza mcikhulupirilo kuti Mpulumutsi adzadza tsiku lina.

## CIPANGANO - MPULUMUTSI WAFIKA

Cipangano ca Tsopano cikwaniritsa mau a Cipangano ca Kale. Pa nthawi yabwino, mpulumutsi anafika. Paulo analemba nati, "Koma pokwanira nthawi, Mulungu anatuma Mwana Wace, wobanda ndi mkazi, wobadwa wakumvela lamulo; kuti akaombole iwo akumvela lamulo, kuti ife tikalandile umwana." Agalatiya 4:4,5. Cikwuaniritso ca lonjezo la mpulumutsi cilankhulidwa motere mCipangano ca Tsopano.

1. <u>Kulalikila ndi kubadwa kwa Yesu</u>.

Mngelo anaoneka kwa Yosefe ndi kumuuza kuti Mariya adzakhala amace wa Mpulumutsi. "Ndipo adzabala mwana wamwamuna; (Mariya) ndipo udzamucha dzina lace Yesu. Pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ace ku macimo ao. Mateyu 1:21. Mulungu anapatsa mwana wace dzina <u>Yesu</u>. Dzina ili liri ndi tanthauzo monga buku la mcipangano cakale <u>Yoswa</u>. Litanthauza "Yehova Mpulumutsi." Litanthauza kuti Mulungu Mpulumutsi. Tsono dzina lakuti <u>Yesu</u> litanthauza kuti Mulungu anatuma mpulumutsi wa anthu ace. Monga mwa Mau a Mngelo, Mariya anabala Yesu. Yesu anabadwa modyela n'gombe ku Betelehemu cifukwa kunalibe malo a Mariya ndi Yosefe mu mzinda muja cifukwa anthu anali ambili. (Werengani Luka 2:6,7). Tidziwa zocepa za ubwana wa Yesu. Tingouzidwa kuti Yesu anakula nakhala wamkulu monga ana ena. "Ndipo Yesu anakulabe m'nzelu ndi mu nsinkhu ndi mcisomo ca pa Mulungu ndi ca pa anthu." Luka 2:52.

2. <u>Ciphunzitso campulumutsi ndi macilitso</u>.

Mulungu anakonza zonse zobwela kwa Mwana wace.



PHUNZILO 10

## KUKHALA M'DZIKO LA MALONJEZANO

BUKU LA PHUNZILO: Yoswa 24:1-18.

<u>VERSI LA PAMTIMA</u>: "Mudzisankhile lero amene mudzamtumikila, - koma ine ndi a m'nyumba yanga, tidzatumikila Yehova." Yoswa 24:15.

Sabata lino tidzaphunzila mbili ya mtundu wa Aisrayeli, pokhala kuti unagonjetsa ndi kulandila dziko limene Mulungu ana'lonjeza iwo tidzakhala tili kulingirila nthawi yaikulu, zaka zoposapo pang'ono cikwi cimodzi. Mbiri iyi ya mtundu ili kupezeka mcipangano cakale kucokera buku la Yoswa mpaka Malaki.

## KUKHALA NDI DZIKO

Buku la Yoswa liyamba ndi Aisrayeli atamanga misasa patsidya la mtsinjewa Yordano. Mose atafa ndipo Yoswa atasankhidwa Kukhala mtsogoleri. Mu versi 5 la buku loyamba tipeza Mulungu ali kumlimbikitsa Yoswa ndi mau awa: "Palibe munthu adzadzakaima pamaso pako masiku onse a moyo wako; monga ndinakhala ndi Mose momwemo ndidzakhala ndi iwe; sindidzakusowa, sindidzakusiya."

Ndipo Mulungu anauza Yoswa m'mene mtsinje wa Yordano udzaolokedwa pogonjetsa dzikolo. Ayenela kuwaononga onse anthu a m'dzikolo. Powelenga lamulo ili, cionekc ngati mau opanda cifundo ocokakwa Mulungu wa cikondi. Koma tiyenela kukumbukila ici: Anthu aku kanani anali ocimwa kwambili. Zaka zikwi zambili nthawi iyi isanafike, pamene Mulungu analonjeza dzikolo kwa Abrahamu ndi anthu ace, Mulungu anati padzakhala nthawi yakuyembekeza, "Pakuti mphulupulu za Aamori sizinakwaniridwe." Genesis 15:16b. Tsopano anakhala ocimwa kwambili kuti kunalibe ciyembekezo ca iwo. Mu nzelu za Mulungu Kunali kwabwino iwo kuonongedwa pamaso a dziko la pansi. Cifukwa cace Mulungu analamulira ana Aisrayeli kuononga anthu onse a dziko limene anali kulowamo. Mulungu anawacenjeza kuti

3. Mulungu analonjeza mpulumutsi. Tiona lonjezano iri lokwaniritsidwa mwa Kristu Yesu.

Pakati pa sabata phunzirani maina asanu a m'Buku Lopatulika. Ndi awa Genesis, Eksodo, Levitiko, Numberi, Deuteronomo.

Mwakuphunzila kwanu werengani mabuku awa:-

Genesis 1 - 3; Genesis 12: 1-3; Genesis 37 - 47; Eksodo 1 - 13; Eksodo 20:1-17; Numeri 13 - 14.

-ooOoo-



Asanabadwe Yesu, mwana wina anabadwa wochedwa Yohane Mbatizi. Yohane anakula mcipululu Kumene anali yekha ndi Mulungu. Atakula, Mulungu anamutsogolera kulalikira za kubwela kwa Yesu ndi kuitana anthu kulapa. Anthu atalapa, Yohane anawabatiza; cifukwa cace anachedwa Yohane Mbatizi Yohane Mbatizi anakonzela njira ya Yesu. Tsiku lina pamene Yohane anali kulalikila pafupi ndi mtsinje wa Yordano, Yesu anadza ndipo anabatizidwa ndi Yohane. (Werengani Mateyu 3:13-17). Momwemo Yesu anauza anthu kuti adzacita cifuniro ca Atate wace wa kumwamba. Ndipo anayamba kulalikila kuitana ophunzila ace. "Yesu anadza ku Galileya, nalalikira uthenga wabwino, wa Mulungu, nanena, nthawi yakwanila, ndipo Ufumu wa Mulungu wayandikila; tembenukani mtima, khulupirilani uthenga wabwino." Marko 1:14,15.

Zaka zokwanila zitalu za m'moyo wa Yesu analalikira kwa anthu, anacilitsa odwala ambili ndi opuwala, ndipo anaphunzitsa ophunzila ace mau ace.

3. <u>Imfa ndi kuuka kwa Mpulumutsi</u>.

Yesu anadziwa cifukwa anabwelera padziko la pansi. Anadza kupulumutsa ocimwa. Pocita ici, anafa pa mtanda cifukwa ca ife. Paulo analemba kwa a Kristu ena kuwakumbutsa za uthenga woona wa cipulumutso. Anati, "Ndipo ndikudziwitsani, abale, uthenga Wabwino umene ndinakulalikilani inu.......Kuti Kristu anafera zoipa zathu, monga mwa Malembo. 1 Akorinto 15:1-3. Ndiponso Paulo analemba, "Mulungu atsimikiza kwa ife cikondi cace ca mwini yekha. M'menemo kuti, pokhala ife cikhalile ocimwa Kristu adatifera ife." Aroma 5:8. Yesu analankhula za Iye yekha, "Pakuti ndithu, Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa, koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la kwa anthu ambili." Marko 10:45. Inde, Yesu anatifera. Koma sicomweco ai. Yesu ali wa moyo tero cifukwa anaukitsidwa kwa akufa ndi mphamvu ya Mulungu. Polankhula za imfa ya Yesu, Paulo anatinso, "Ndi kuti anaikidwa, ndi kuti adaukitsidwa tsiku lacitatu monga mwa malembo." 1 Akorinto 15:1-4. Inde, Yesu ali moyo. Tipemphera ndikutumikila Mpulumutsi wa moyo.

4. Lamulo la Mpulumutsi wa Moyo.

Pamene Yesu anaukitsidwa kwa akufa. Anakumana ndi ophunzila ace kwambili. Nthawi yotsiriza anakumana naye asanakwere kumwamba. Anawapatsa lamulo. Mateyu analemba lamulori mbuku lace. "Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndikuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo anati Ine ndili pamodzi ndi inu masiku onse, Kufikila cimaliziro ca nthawi ya pansi pano. Mateyu 28:19,20. Yesu analamulira ophunzila ace kuuza anthu mbiri ya bwino, Kuyamba buku la Macitidwe ndi mbiri ya ophunzila a Yesu ali kumvera lamulo la Mpulumutsi. Lamulo la Yesu liri ndi nchito ziwili. (1) Kupanga ophunzila ndipo (2) Kuphunzitsa ophunzila.

Ophunzila oyamba a Yesu anali omvera Iye. Kodi tiri kumvela lamulo la Mpulumutsi?

KUTSILIZA: Buku lonse lopatulika liri mbiri yakudzanso kwa Mpulumutsi, Yesu Kristu, Mwana wa Mulungu. Alembi a Cipangano cakale analonjeza Kuti Mpulumutsi adzabwela. Alembi a Cipanano ca Tsopano akamba za kudza kwa Yesu ndipo m'mene anamphela ndi kuukanso kwace. Ndipo anenanso za m'mene ophunzila oyamba a Yesu anauzila anthu mbili yabwino ya Mpulumutsi.

Tiziphunzila Buku Lopatulika Kuti tidziwe zambili za Yesu ndi u'funiro wace pa miyoyo yathu.

-ooOoo-





Mose ndi mbale wace Aroni anapita kwa mfumu ya Aigupto, Farao. Anamuuza kuti Mulungu ananena kuti, "Lolani anthu anga apite." Farao anakana. Mulungu anatumiza cilango kwa anthu amu Aigupto cifukwa Farao sanamvera. Kawiri ndi kawiri Mose ndi Aroni anafunsa Farao lora a Israyeli kucoka mu Aigupto. Anakanabe. Mulungu anapitirilabe kutuma zozizwitsa. Potsiriza Farao analora Aisrayeli kuturuka mu Aigupto.

## CIYAMBI CA CIKONZEDWE CA DZIKO LA MALONJEZANO

Anatha zaka zambiri kuyenda m'cipululu asanalowe m'dziko limene Mulungu anawalonjeza. Pa nthawi iyi, zinthu zambili zinacitika. Anthu analema ndikuyenda m' cipululu. Nthawi zambili analikufuna kubweleranso ku Aigupto. Mulungu anawasamalira. Anawapatsa madzi ndi cakudya.

Mulungu anadziwa kuti anthu awa anafunika malamulo akuwatsogolera. M'moyo wao. Anaitana Mose kupita ku phiri kukalandila malamulo. Mulungu anapatsa Mose Malamulo khumi ndi malamulo ena. Tipeza Malamulo Khumi mu Eksodo 20:1-17a.

Nthawi ina, Mulungu anali okonzeka kutsogolera ana a Israyeli ku dziko la malonjezano. Mose anafuna amuna khumi ndi awiri kudzikolo kukaona m'mene dziko lilili. Pamene anabwelera, anthu khumi anati sakhoza kugonjetsa dzikolo. Anthu anali akulu akulu. Ncosatheka. Awiri a iwo anati, ndi mphamvu ya Mulungu akhoza kugonjetsa dzikolo. Cifukwa cace Mulungu anati ayenela kuyendanso m'cipululu kwa zaka makumi anai. Ndipo alowe m'dziko la malonjezano.

Pali zinthu zina tiyenera kuphunzira muphunziro ili.

1. Mulungu analenga zinthu zonse. Analenga inu.

2. Monga Adamu ndi Hava, tonse tinacimwa ndi kusamvera Mulungu. Tiyenera kupulumutsidwa.

fai, cifukwa adziwa Mulungu. Kuti tsiku limene mukadya umenewo, adzatseguka maso anu, ndipo mudzakhala ngati Mulungu, wakudziwa za bwino ndi zoipa. Genesis 3:4,5.

Hava anayang'ana mtengowo. Zipatso zinaoneka zabwino. Ndipo anatenga zipatso za mtengowo nadya. Ndipo anapatsa zina kwa mwamuna wace Adamu.

Posacedwa anadziwa kuti anacita cimene Mulungu anawalamulira kuti asacite. Anacimwa. Cimo linalowa m' dziko lokongola limene Mulungu analipanga.

Momwemo, cifukwa ca cimo panali lonjezo. Mulungu anati, "Ndipo ndidzaika udani pakati pako (kunena kwa njoka) ndi mkazi, pakati pa mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira citende cace." Genesis 3:15. Mulungu analonjeza kuti adzatumiza Mpulumutsi pa dziko lapansi.

## CIYAMBI CA MTUNDU WOSANKHIDWA

Zaka zambiri zinapita. Anthu ambiri analinkukhala pa dziko. Munalinso ucimo woculuka m'dziko lapansi. Mulungu anaitana Abramu kukhala atate wa anthu ace osankhidwa. (Werengani Genesis 12:1-3). Abramu anamvera Mulungu. Mulungu anamudalitsa kwambiri. Mulungu analonjezanso kutuma mpulumutsi ku dziko lapansi.

## CIYAMBI CA UKAPOLO

Patapita zaka zambiri, njara inafika pa dziko lonse. Koma ku Aigupto kunali cakudwa cambiri. Mulungu anapatsa osankhidwa ace kupyolera mwa Yosefe, m'modzi wa mbadwo wa Abramu. Mulungu analora Yosefe kukonzeratu cakudya ca njara iyi. Pamene njala isanathe, Aisrayeli (anthu osankhidwa a Mulungu) anapita ku Aigupto.

Zaka zambiri zitatha, Aisrayeli anakhala akapolo a Aigupto. Anabvutika kwambili pa nthawi iyi. Mulungu anamva kurila kwao pofuna kupulumutsidwa. Ndipo anatuma Mose kuwaturutsa m'dziko la Aigupto kufika kudziko limene Mulungu adzawapatsa.



PHUNZILO 4

## CIPANGANO - CILANKHULA KWA IFE LERO

BUKU LA PHUNZILO: 2 Timoteo 3:14-17; Masalmo 119:9-11.

VERSI LA PAMTIMA: "Ndinawabisa mau anu mumtima mwanga, kuti ndisalakwire inu." Masalmo 119:11.

"Pakuti mau a Mulungu ali a Moyo, ndi ocitacita, ndi akutwa koposa lupanga lakutwa konse konse, ......nazindikiritsa zolingirila ndizitsimikizo za mtima." Ahebri 4:12.

## CIPANGANO - COGAWA ANTHU

Kodi muganizanji za cipangano? Ena anganene, "Cipangano ndi buku la bwino koma ndimangosalimvela." Kunena kwa mtundu uyu ku tanthauza kuti munthu sadziwa Cipangano. Popeza ngati munthu awelenga Cipangano ndi mtima onse, adzakhala ndi cinthu cimodzi kapeza ziwili pa za Cipangano. Adzakonda Cipangano kapena adzacida. Popeza Cipangano cilankhula monga anthu alili ndipo ndi kuwadziwitsa kuti ali ocimwa. Ndipo Cipangano ciuza anthu cimene angakhale mwa Yesu Kristu.

## CIPANGANO - UTHENGA WA MOYO

Cipangano cisiyana ndi mabuku ena. Uthenga wa Cipangano sukalamba. Cipangano cili ndi uthenga umene anthu onse afuna azaka zosiyana ndi mibadwo yosiyana. Cipangano cili ndi uthenga wa Moyo. Yesu anati, "Ndi mzimu umene ufulumizitsa, thupi siliphindula: mau amene ndi lankula ndi inu, ali mzimu, ndipo ali moyo." Yesu anali Kutiuza kuti mau ace akhoza kutipatsa ife moyo ngati tidzanva ndi kumvela. Inde, Cipangano cili buku la moyo. Ciri kukhala ndi kucitacita popeza ciri Mau a Mulungu wamoyo. "Pakuti mau a Mulungu ali amoyo, ndi ocitacita." Ahebri 4:12. Petro analemba za Cipangano kuti "Mwa mau a Mulungu a moyo ndi okhalitsa." 1 Petro 1:23. Zitsanzo zimene zapatsidwa pokamba za Cipangano zionetsa kuti muli uthenga wamoyo. Yesu anati, "Mbeuzo ndizo mau a Mulungu."

Luka 8:11. Masalmo ati, "Mau anu ndiwo nyali yakumapazi anga. Ndikuunika kwa panjila panga." Masalmo 119:105. Mneneri Yeremiya anati, "Kodi mau anga safanana ndi moto? ati Yehova" Yeremiya 23:29. Paulo analinganiza mau a Mulungu ndi lupanga. "Ndi lupanga la mzimu, ndilo mau a Mulungu." Aefeso 6:17. Zitsanzo zonsezi zitsimikizila kuti cipangano ndi buku la moyo ndi locitacita.

## CIPANGANO - CILANKHULA KWAIFE

Cipangano cimalankhula kwa ife zazikulu za moyo.

1. Cipangano cilankhula kwa ife za cipulumutso.

Paulo analembela kwa Timoteo za mphamvu yotionetsa ife cipulumutso. ".....Ndi kuti kuyambila ukhanda wako wadziwa malembo opatulika, okhoza kukupatsa nzelu kufikila cipulumutso. Mwacikhulupirilo ca mwa Kristu Yesu." 2 Timoteo 3:15. Cipangano cimatiuza Kuti tikhoza kupulumutsidwa kumacimo athu. Citiuza m'mene tingadziwire Mulungu. Cifuniro cacikulu ca munthu ndiko kudziwa Mulungu. Kodi mufuna kudziwa Mulungu? Kodi mufuna kukhulupirila mwa Yesu Kristu? Paulo analemba nati, "Comweco cikhulupirilo cidza ndi mbiri, ndi mbiri idza mwa mau a Kristu." Aroma 10:17. Ngati mufuna kudziwa Mulungu muyenera kuphunzila Cipangano.

2. Cipangano citiphunzitsa kukhala mwa Yesu pano padziko la pansi.

Pamene munthu akhulupirila mwa Yesu Kristu ndipo adziululira kwa anthu, wangoyamba umoyo wa ci Kristu. Pali zinthu zambili zimene m'Kristu watsopano ayenela kudziwa. Moyo wa ci Kristu ndiko kutsata Yesu tsiku ndi tsiku. Uku ndiko kuti moyo wonse wa munthu. Yesu anati, "Ngati munthu afuna kudza pa mbuyo panga, adzikane yekha, nanyamule mtanda wace tsiku ndi tsiku, nanditsate ine." Luka 9:23. M'Kristu adzayesetsa kutsata Yesu tsiku ndi tsiku. Njila yakuphunziliramo kumvela Yesu ndi pa Kuphunzila Cipangano.



PHUNZILO 9

## CIYAMBI

BUKU LA PHUNZILO: Genesis 1:1-31; Eksodo 20:1-17.

VERSI LA PAMTIMA: "Paciyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko la pansi." Genesis 1:1.

### CIYAMBI CA OZIKO

Mu Genesis 1:1 tiwerenga mau awa: "Paciyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko la pansi." Mulungu analipo dziko lapansi silinapangidwe. Analenga kuwala ndi mdima. Kumene anacha "usana" ndi "usiku." Ndipo analenga thambo, limene anacha kumwamba. Pambuyo pace analenga mtunda, nyanja, udza, mitengo ndi zomela zina. Analenga dzuwa, mwezi ndi nyenyezi. Ndipo anapanganso moyo wa zolengedwa za dziko lathu - nsomba, nkhuku, ndi nyama zonse.

### CIYAMBI CA MUNTHU

Potsiriza Mulungu analenga munthu. Tiwerenge Genesis 1:26. "Ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m' cifanizo cathu, monga mwa cikhalidwe cathu." Genesis 1:26a. Mulungu anaona kuti sicinali ca bwino munthu kukhala yekha. Motero anapanga mkazi kukhala wosangalatsa ndi kuthandiza Adamu.

### CIYAMBI CA UCIMO NDI CIYEMBEKEZO

Adamu ndi Hava, mwamuna ndi mkazi woyamba amene Mulungu analenga, anakhala m'munda wabwino wa Eden. Mulungu anawauza kudya zipatso za mtengo uli wonse koma umodzi wokha asadye. Mtengowo unali mtengo wakudziwitsa za bwino ndi zoipa. Mulungu anati, "Tsiku limene mudzadya za mtengowo mudzafa." Genesis 2:17b.

Patapita nthawi, satana anafika kwa Hava. Anaonekera mwa njoka. Njokayo inafunsa Hava za lamulo la Mulungu. "Njokayo ndipo inati kwa mkaziyo, kufasimudza-

Mulungu afuna ife kucita kanthu kena kuti tilandile mphatso ya cimwemwe cimene Iye atilonjeza.

Dzazani malembo m'malo awa. "Kufikila tsopano simunapempha kanthu m'dzina langa:_____________ ndipo _________________, kuti _________________ cikwaniridwe." (Yohane 16:24).

-ooOoo-



3. Cipangano citiphunzitsa kukhala anthu abwino a dziko lathu.

Kodi m'Kristu ayenela kugwapo pa ndale za dziko? Kodi ayenela kusankha a bwalo la malamulo? Cipangano ciyankha, inde. Paulo analemba kuti, "Anthu onse amvele maulamuliro a aKulu; pakuti palibe ulamuliro wina koma wacokera kwa Mulungu: ndipo iwo amene alipo aikidwa ndi Mulungu." Aroma 13:1. Yesu anati, "Patsani kwa kaisara zace za Kaisara, ndi kwa Mulungu zace za Mulungu." Mateyu 22:21. Pamene Yesu analankhula za Kaisara, anali kufanizila ku boma la masiku aja. Yesu anali kunena kuti tili ndi zopeleka za boma popeza boma ndi la nchito ya anthu onse. Ndipo ananenanso kuti tili ndi zopereka za Mulungu. M'Kristu ayenera kudziwa kuti cikondi cathu ca pa Mulungu ciyenela kukhala coposa ca pa boma lathu ndi pa dziko lathu. Popeza Mulungu anapanga dziko lathu ndi kulora boma kukhalapo. M'Kristu ali yense ayenera kumvera malamulo a boma lace. Koma iwo amene akana kumvela malamulo a Mulungu sibwino kuwamvela. M'Kristu ayenera kumvera Mulungu poyamba. Cifukwa cace, palibe kusiyana kukhala mKristu wa bwino ndi kukhala mkhalidwe wabwino.

4. Cipangano cilankhula Kwaife za kukula kwace kwa banja ndi mpingo.

Banja ndi mpingo zili pamodzi. Banja liri lonse liyenera kukhala la ci Kristu. Atate ndi amai ayenela kuuza ana ao Kudziwa Mulungu. Banjalo liyenera kupita ku Chalici pamodzi kukapemphera pa sabata liri lonse. Mulungu anayamba banja ndi mpingo.

5. Cipangano cilankhula za moyo titafa.

Kodi muopa kufa? MKristu sayenera kuopa kufa popeza Yesu, Mpulumutsi wathu, anapambana imfa. Yesu anaukitsidwa kwa akufa. Ali ndi Moyo lero ndipo analonjeza moyo wosatha kwa onse omkhulupirila Iye. Yesu anati, "Ine ndine kuuka ndi moyo, wokhulupirila ine ngakhale amwalira, adzakhala ndi moyo: ndipo yense wakukhala ndi moyo, nakhulupirila ine sadzamwalira nthawi zonse." Yohane 11: 25,26. Pali ma versi ena ambili amene alonjeza moyo kwa

mKristu atafa. Abwino koposa ali pa 1 Akorinto 15:12-58. Werengani ma versi awa pamene muli kuphunzila Cipangana Inde, Cipangano citsimikizila mKristu ali yense kuti imfa sindiko kutha kwa moyo ai. Imfa ndiyo khomo la mKristu kulowa ku mwamba ndi kukhala ndi Yesu nthawi zonse.

KUTSILIZA: Cipangano ndi codabwitsa. Cimalankhula kwa munthu ali yense amene adzamva. Cili ndi uthenga umene anthu onse afuna. Palibe amene amaphunzila mokwanila kuti angaleke kuphunzila. Cifukwa cace, tiyeni tidzipereke kuphunzila Cipangano nthawi yonse.

"Ucite cangu Kudzionetsela kwa Mulungu wo bvomerezeka, wanchito wopanda cifukwa cakucita manyazi, wolunjika nao bwino mau a coonadi." 2 Timoteo 2:15.

-ooOoo-



mphatso, moyo wosatha. Pamene tikhala ana a Mulungu, ndife ana aMulungu kunthawi zonse. Pa versi ili tiona kuti tiyenela Kucita kanthu kuti tilandile mphatso yaikulu ya cipulumutso.

Dzazani malembo m'malo awa. "Iye ______________ mau anga, ndi ______________ Iye amene ananditumа ine, ali nao ________________, ndipo salowa mkuweruza, koma wacokera ku imfa, nalowa m'moyo." (Yohane 5:24).

Pano tiona kuti munthu ayenela kumva Mau a Mulungu. Cifukwa cace tiyenela kuphunzila Cipangano cathu. Coyamba, tiyenela kumva cimene Mau a Mulungu anena kwa ife. Koma kungokumva Mau a Mulungu kulibe phindu. Munthu ayenela kukhulupirila, kukhulupirila kucoka mkuwerenga Mau a Mulungu ndi kupemphela kwa Mulungu, amene anatuma mau ace. Inde, pamene munthu amva mau a Mulungu ndi kukhulapirila mau a Mulungu alandila Yesu Kristu. Timati munthu ali ndi moyo wosatha ndi Mulungu. Ili ndi lonjezo kwa onse amene adzakhulupirila.

5. MZIMU WOYERA: LONJEZO NDI MPHATSO YA MULUNGU.

Tsegulani pa Macitidwe 2:38,39. Pano tiona kuti Mulungu afuna ife kucita zinthu zina kuti tilandile mphatso yace.

Dzazani malembo m'malo awa. "______________ ______________ Yense wa inu m'dzina la ______________ kuloza ku cikhululukiro ca Macimo anu, ndipo mudzalandila mphatso ya ________________." (Macitidwe 2:38,39).

6. CIMWEMWE: LONJEZO NDI MPHATSO YA MULUNGU

Tidzawelenga pamodzi buku la Yohane 16:24 ndi Masalmo 16:11. Mu Yohane 16:24 tiphunzila kuti popemphela m'dzina la Yesu Kristu tidzalandila zinthu zija zimene Mulungu adziwa zili zotiyenela. Zinthu izi zimene Mulungu afuna kutipatsa zidzabweletsa cimwemwe. Komanso,

Dzazani malembo m'malo awa. "Ngati__________ macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye __________macimo athu, ndi__________ kuti cotsela cosalungama ciri conse." (1 Yohane 1:9)

Pano tiona kuti Mulungu ali afuna kutikhululukila macimo athu ngati ife coyamba tibvomereza macimo athu kwa Iye.

2. CIFUNDO: LONJEZO NDI MPHATSO YA MULUNGU.

Titsegule pa buku la Yesaya 55:7. Pano tionanso kufuna kwa Mulungu kutipatsa mphatso ina. Mphatso ya cifundo ndi mphatso yaikulu yacoka kwa Mulungu. Koma tionanso kuti pali zinthu zina zimene tiyenela kucita pamene Mulungu aKalibe kuticitila cifundo.

Dzazani malembo m'malo awa. "Woipa__________ njila zace, ndi munthu wosalungama asiye__________ __________:__________kwa Yehova, ndipo Yehova adzamcitira cifundo; ndi kwa Mulungu wathu, pakuti Iye__________koposa." (Yesaya 55:7)

3 CIPULUMUTSO: LONJEZO NDI MPHATSO YA MULUNGU.

Tsopano titsegule pa buku la Aroma 10:9. Pano tiona kuti Mulungu amafuna kutipatsa mphatso ina, cipulumutso. Monga tili kuwerenga pamodzi tidzaphunzila kuti Mulungu afuna ife kucita kanthu poyamba. Mu versi ili Mulungu afuna ife kulandila mphatso yaikulu ya cipulumutso.

Dzazani malembo m'malo awa. "Kuti ngati__________ __________m Kamwa mwako__________ndi __________ mumtima mwako kuti Mulungu__________kwa akufa, __________." (Aroma 10:9). Werenganinso Luka 13:3 ndi Macitidwe 20:21.

4. MOYO WOSATHA: LONJEZO NDI MPHATSO YA MULUNGU.

Titsegule pa buku la Yohane 5:24. Pano tiphunzila za



PHUNZILO 5

MAGAWO AWILI A BUKU LO PATULIKA NDI ZIPHUNZITSO ZAO

BUKU LA PHUNZILO: 2 Timoteo 3:16; Yohane 5:39; Luka 24:27; 2 Petro 1:21; Yesaya 53.

VERSI LA PAMTIMA: "Koma zalembedwa izi Kuti mukakhulupirile kuti Yesu ndiye Kristu Mwana wa Mulungu ndi kuti pakukhulupira mukhale nao moyo m'dzina lace."
Yohane 20:31.

MAGAWO AWIRI ABUKU LATHU LOPATULIKA

CIPANGANO CAKALE. Tiyeni titsegule zipangano zathu patsamba loyambilira. Pano tipeza maina awili atali. Pamwamba pa maina oyamba tipeza mau olembedwa 'Cipangano Cakale'. Pansi pa mau awa tipeza mabuku 39. Awa achedwa mabuku a Cipangano cakale. Genesis ndilo buku loyamba la Cipangano Cakale. Tsopano tiyeni tisanthule matsamba kufikila titapeza buku la Malaki. Tiyeni tiike dzanja lathu la manja pompano pamene dzanja lathu la manzele liri poyamba pa Buku Lopatulika. Tsopano tagwila m'manja mwathu gawo loyamba la Cipangano Cipangano ca Kale. Gawoli loyamba linalembedwa zaka zambili zitapitapo pamene gawo laciwiri lisanalembedwe.

CIPANGANO CA TSOPANO: Tsopano tidzasanthula matsamba a Cipangano ca kutsogolonso. Tiyeni tione maina ena a mabuku. Pano tipeza dzina 'Cipangano Ca Tsopano.' Muli mabuku 27 m'Cipangano ca Tsopano. Tiyeni tipeze buku la mateyu pamodzi. Mateyu ndilo buku loyamba la Cipangano ca Tsopano. Tiyeni tiike dzanja la manzele pompano, ndiponso tiike dzanja lathu la manja potsilizila pa Cipangano. Tsopano tagwila gawo laciwili la Buku Lo Patulika Buku la Cipangano catsopano linalembedwa zaka zambili zapitapo atalemba cipangano cakale.

CIPANGANO CAKALE NDI CATSOPANO NDI CIMODZI

Taona Kuti tili ndi magawo awili a Buku Lopatulika. Tiyenera kukumbukila kuti magawo awili awa apanga buku

limodzi, Cipangano. Sitingati dela limodzi nlofunika koma linanso ai. Ngati mulandila kalata ocokera kwa atate wanu ku mudzi ndi matsamba ena ocokako mukhoza kufuna matsamba aja ena amene anasowa. Cifukwaninji? Popeza dela lina lifunika kuti inu mumve uthenga onse ocokela kwa atate wanu. Cimodzi modzi, Cipangano ca Kale ndi Catsopano zifunika kuti uthenga wa Mulungu wakwa anthu onse umvetsedwe. Inde, ngakhale Cipangano cathu cili ndi madela awili, ciKamba mbili imodzi.

## UTHENGA WA MULUNGU

Uthenga wa Mulungu wa kwa anthu onse upezedwa m' Cipangano, Mau a Mulungu. Pamene tiphunzila Cipangano, tikhoza kupeza kuti uthenga wa Mulungu ndi wogawidwa pawiri.

1. Lonjezo la Mulungu kwa dziko la pansi. Cipangano cakale cikamba za lonjezo la Mulungu za Yesu Kristu. "Taonani namwali adzaima, nadzabala mwana wa mwamuna, nadzamucha dzina lace Imanueli." Yesaya 7:14.
2. Mphatso ya Mulungu ku dziko. Cipangano ca Tsopano cikamba za Yesu, pakudza kwace. "Ndipo pakubadwa kwace kwa Yesu mBetelehemu wa Yudeya m'masiku a Herode mfumu, onani, Anzelu aKum'mawa anafika ku Yerusalemu, nati, Ali kuti amene wabadwa Mfumu ya Ayuda? Cifukwa tinaona nyenyezi yace ku m'mawa, ndipo tinadzela Kudzamlambila Iye." Mateyu 2:1-2. Pano taphunzila zinthu zazikulu ziwili. Coyamba, Mucipangano ca Kale tiwelenga za lonjezo la Mulungu pa Kudza kwa mwana wace padziko lapansi. Caciwiri, mCipangano ca Tsopano tiwerenga kudza kwa Mwana wace, monga analonjezedwa ku dziko lapansi.

## LONJEZO LA MULUNGU

Muphunzilo lathu la lero tidzayesa kuphunzila zambili za lonjezo la Mulungu. Sabata la mawa tidzaphunzila pamodzi zinthu zambili za mphatso ya Mulungu.

Tiyenela Kudziwa, coyamba, kuti Mulungu ndi wamphamvu zonse. Ali ndi mphamvu zakucita zinthu zonse.



PHUNZILO 8.

## KUSANTHULA MALEMBO NDIKUPEZA MALONJEZO AMULUNGU NDI MPHATSO ZA MULUNGU

BUKU LA PHUNZILO: Mateyu 24:29,30; Yobu 19:25; Yohane 14:16-18; Mateyu 6:14,15; Nehemiya 9:17; Yesaya 45:22; Yohane 5:24; Macitidwe 2:38,39; Yohane 16:24; Mateyu 16:27.

VERSI LA PAMTIMA: "Yesu amene, walandilidwa kunka kumwamba kucokera kwa inu, adzadza momwemo monga munamuona alinkupita kumwamba." Macitidwe 1:11.

## MULUNGU APELEKA MPHATSO ZAMBILI

Lero tidzapeza ma versi a m'Cipangano amene atiuza za mphatso za Mulungu kwa ife. Mulungu alonjeza kwa ombvomeleza mphatso zodabwitsa zambili.

Ife tonse tidziwa kuti mphatso yoposa zonse ndi Yesu Kristu mwana wa Mulungu. Koma pali mphatso zina zimene zingapatsidwe kwa onse amene atsata Mulungu. Tiyeni tikhumbukile kuti ciri conse cimene Mulungu alonjeza, ali okhoza kucicita. "Ndipo poyang'anila lonjezo la Mulungu sanagwedezeka cifukwa ca kusakhulupirila, koma analimbika m'cikhulupirilo, napatsa Mulungu ulemu, nakhazikikanso mumtima kuti, cimene Iye analonjeza, anali nayonso mphamvu yakucicita." Aroma 4:20,21.

1. CIKHULULUKIRO: LONJEZO NDI MPHATSO YA MULUNGU.

Tiyeni titsegule pa buku la 1 Yohane 1:9. Pano tiphunzila m'mene tingakhululukidwile macimo athu. M'mene tili kuona pa versi ili tiona zinthu ziwili. Pali cinthu cimene tiyenela kucita ndi cimene Mulungu ayenela kucita.

anakomana pamodzi kupemphera. Buku Lopatulika linena kuti anali onse a mtima umodzi pamene anali kupemphela Mulungu. Tikhoza kuzindikila kuti Mulungu adzafika m'mitima yathu ngati tisonkhana pamodzi ndi kupemphela moona.

## CIANI CICITIKA NGATI AKRISTU APEMPHERA PAMODZI MONGA MWA LONJEZO LA MZIMU WOYERA

Pamene anthu abwela pamodzi kupembedza Mulungu adzampeza Iye, ngati mapemphero ao ali oona. "Koma mukafuna Yehova Mulungu wanu Kumeneko, mudzampeza, ngati mumfunafuma ndi mtima wanu wonse ndi moyo wanu wonse." Deuteronomo 4:29.

1. Pamene anthu alola mzimu Woyera kulowa m'mitima yao, amafunsa, "Tidzacita ciani." Werengani Macitidwe 2:37. Pano anthu anasonkhana pamodzi m'mapemphero ndipo Petro analalikira za Yesu. Mzimu Woyera unadza m'mitima yao. Anamva kuti ayenela kucita kanthu. Ngakhale leronso pamene Mzimu Woyera ukolowa m'mitima ya anthu, kulikonse pa dziko la pansi, anthu aja amafuna kudziwa, "Kodi tidzacita ciani."

2. Funso lifunsidwa, "Mulungu amafuna ife kuti ticite ciani?" Werengani Macitidwe 2:38. Pano tiona kuti Petro ayankha funso ndi mau akuti lapani. Werenganinso Luka 13:3. Koma cinthu cina ndi cofunika, Tiyenela kukhala ndi cikhulupirilo mwa Yesu Kristu. Tiyenela kubvomereza Yesu m'mitima yathu mwa Cikhulupirilo. Werengani Macitidwe 20:21.

3. Ngati anthu asonkhana pamodzi m'mapemphero kufuna Mulungu ampeza Iye Anthu amasendela pafupi ndi Mulungu. Mulungu amasendela pafupi ndi anthu. Pamene ici cicitika anthu amakhala pafupi ndi anzao. Werengani Macitidwe 2: 44-47.

-ooOoo-



Ndiponso Mulungu ali ndi nzelu zonse. Cifukwa cace, ngati alonjeza cinthu pali ku funika kwa cinthuco. Pamene Mulungu ati lonjeza kanthu, tiyenela kudziwa kuti adzasunga lonjezano lace.

## LONJEZO LA MULUNGU - CIYEMBEKEZO CATHU

Nthawi ya m'Cipangano ca Kale ndi mbili ya ciyembekezo ca nthawi imene Mulungu adzafika ku dziko la pansi kudzapulumutsa dziko kumacimo. Atumiki a Mulungu monga Yesaya ndi Yoweli, anauzidwa Kuuza dziko lonse za lonjezo lalikulu la Mulungu kwa dziko la pansi. Mulungu anafuna kubwela pa dziko mwa Mwana wace. "Pakuti kwa ife mwana wa khanda wabadwa kwa ife mwana wamwamuna wapatsidwa; ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa lace, ndipo adzamucha dzina lace Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu wamphamvu, Atate Wosatha, Kalonga wa Mutendere." Yesaya 9:6.

## CIFUKWA CA LONJEZO LA MULUNGU

1. Kugwa kwa munthu. Ucimo unalowa pamitundu ya anthu mwa Adamu ndi Hava, makolo athu oyamba. Ici citsimikiza kuti munthu ali yense padziko anacimwa. "Pakuti onse anacimwa napelewela pa ulemelero wa Mulungu." Aroma 3:23. Munthu anagwa pogwilizana mu Mzimu ndi Mulungu. Anafa, mumzimu, cifukwa ca ucimo wa Adamu. "Pakuti monga mwa Adamu onse amwalira." 1 Akorinto 15:22.

2. Ucimo uyenela kulipidwa. Ucimo sudzakhala osalangidwa, Munthu wina ayenela kuyankhila ucimo. Anthu mCipangano ca Kale anali kupeleka zoweta paguwa cifukwa ca macimo. Koma tidziwa kuti zoweta sizikhoza kukhululukila macimo, koma Mulungu yekha. Anthu onse, cifukwa ca ucimo, ayenela kufa. "Pakuti mphoto yace ya ucimo ndi imfa." Aroma 6:23.

3. Munthu anayenela kupulumutsidwa ku ucimo ndi imfa. Munthu sanakhoza kucita ciri conse kudzipulumutsa ku macimo ndi imfa. "Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupirilo, ndipo ici cosa-

cokera kwa inu ciri mphatso ya Mulungu; cosacokera ku nchito, Kuti asadzitamandire munthu ali yense."

Aefeso 2:8,9.

4. Kufuna kwa Mulungu kwaonetsedwa mlonjezano lace. Lonjezo la Mulungu liri la kwa anthu onse. "Ndipo kudzacitika Kuti ali yense adzaitana padzina la Yehova adzapulumutsidwa," Yoweli 2:32. Tiyenela kukumbukila kuti tiyenela kuitana lonjezo la Mulungu Tiyenela kubvomeleza Lonjezano lace ndi kulandila mphatso yace, Yesu Kristu. Werengani Yohane 3:16.

-ooOoo-



Lero tidzaphunzila Buku Lopatulika pamodzi. Ndipo dziwani, kuti ngati mulibe Buku Lopatulika muyenela kugula. Tikhala pamodzi ndi Mulungu kupyolera mkuphunzila Cipangano ndi mapemphero. Ndipo munthu ali yense afunika Cipangano.

MALONJEZO A MULUNGU NDIMPHATSO ZA MULUNGU

1. Mwana wa Mulungu. Zoonadi Yesu Kristu ndiye mphatso yoposa zonse. Tiyeni tione ma versi a m' malembo amene atiuza za mphatso yaikulu ya Mulungu. (1) Mulungu analonjeza mphatso yace m Cipangano Cakale. Werengani Yesaya 7:14. Pano tiona Kuti Mulungu analonjeza mwana wace zaka zambili pamene Yesu asanabwele padziko. (2) Mulungu amasunga lonjezano lace. Werengani Mateyu 2:1,2. Pano tiwerenga Mau a Mulungu pa zakubwela kwa Yesu pa dziko la pansi, monga m'mene Mulungu analonjezela zaka zambili zapita m Cipangano ca Kale. Werenganinso Yohane 3:16. (3) Malo a Kubadwa kwa Yesu. Zaka zambili Yesu asanabadwe anthu anthawi ya M cipangano ca Kale analikuwelenga za malo obadwilamo Yesu. Werengani m Cipangano ca Kale. Mika 4:2. Tsopano tatsegulani Cipangano ca Tsopano, ndipo tidzaona pamodzi kuti Mulungu anasunga lonjezo lace monga za malo obadwilamo Yesu. Werengani Mateyu 2:1. Pano tiona malo a kubadwilamo Yesu, monga Mulungu analonjeza. (4) Yesu anafa m'malo mwathu pa mtanda. Werengani m'Cipangano Ca Kale, Yesaya 53:4,5. Panonso, tiona Mau a Mulungu ali kutiuza kuti Yesu adzatenga macimo athu ndi kufa cifukwa ca macimo athu. Tsopano bweraninso ku Cipangano ca Tsopano kuona kukwaniritsa lonjezo kwa Mulungu. Werengani 1 Petro 2:24. Tionanso kuti Mulungu anasunga lonjezo lace. Cifukwa Yesu anadza padziko la pansi. Yesu anafa pamtanda cifukwa camacimo athu.

2. Mzimu Woyera. (1) Mulungu analonjeza Mzimu Woyera. Werengani Miyambo 1:23. (2) Mulungu amasunga lonjezo lace. Werengani Macitidwe 2:38,39 ndi Macitidwe 2:4. Pano pa Macitidwe 2:4 anthu awa

PHUNZILO 7

## KUSANTHULA MALEMBO NDIKUPEZA MALONJEZO AMULUNGU NDI MPHATSO ZA MULUNGU

BUKU LA PHUNZILO: 1 Mbiri 28:9; 2 Mbiri 15:2; Mateyu 6:33; Mateyu 7:7,8; Luka 11:9,10.

VERSI LA PAMTIMA: "Koma mutange mwafuna ufumu wace ndi cilungamo cace, ndipo zonse zimenezo zidzaonjezedwa kwa inu." Mateyu 6:33.

### MULUNGU NDI MALONJEZO ACE

Tikhoza kukhala odziwa nthawi zonse kuti Mulungu amasunga malonjezo ace. Mwina ife sitinakondwele nthawi ina cifukwa ca anzathu amene sanasunga malonjezo ao. Mulungu anaika malonjezo ambili, koma sanaphwanya lonjezo limodzi. "Wolemekezeka ndi Yehova amene anapumulitsa anthu ace Aisrayeli, monga mwa zonse analonjezazo; sanatayika mau amodzi a mau ace onse a bwino, amene analankhula ndi dzanja la Mose mtumiki wace." 1 Mafumu 8:56.

### TIYENERA KUKHULUPIRILA MALONJEZO AMULUNGU

Ngakhale Mulungu ali okhulupirika posunga malonjezo ace, tiyenela kukhala ndi cikhulupirilo mwa Mulungu kuti Iye adzacita cimene alonjeza.

Tiyeni tione cimene cinenedwa za lonjezo la Mulungu ndi cikhulupirilo ca Abrahamu. Coyamba, Abrahamu anakonda Mulungu kwambili. Anaika cikhulupirilo cace mwa Mulungu. Ndipo Mulungu anakonda Abrahamu. Ngakhale kuti Abrahamu anayesedwa nthawi zina, anakhalabe okhulupirika kwa Mulungu. Werengani zimene zinenedwa za cikhulupirilo ca Abrahamu pa Mulungu. "Ndipo poyang'anila lonjezo la Mulungu sangwedezeka cifukwa ca kusakhulupilira, koma analimbika mcikhulupirilo, napatsa Mulungu ulemu, nakhazikikanso mu mtima kuti, cimene Iye analonjeza, anali nayonso mphamvu yakucicita." Aroma 20:21.



PHUNZILO 6

## MPHATSO YA MULUNGU

BUKU LA PHUNZILO: Yohane 3:16-21; Ahebri 1; 1 Timoteo 2:5,6; Yohane 14.

VERSI LA PAMTIMA: "Pakuti Mulungu anakonda dziko la pansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirila Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha." Yohane 3:16.

### MPHATSO YA MULUNGU

Muphunzilo lathu sabata latha tinaphunzilo pamodzi za lonjezano la Mulungu. Lero tidzaphunzila za mphatso ya Mulungu. Tiyenela kumvetsetsa Kuti Mulungu anapatsa malonjezano ambili. Lonjezo lalikulu limene Mulungu analonjeza ndilo loti adzatumiza Mwana wace Yesu Kristu.

Tinaphunzila mu phunzilo lathu lapita kuti anthu a m'cipangano cakale anali kuyembekeza kudza kwa Yesu Kristu. Lero tiphunzila m'cipangano ca Tsopano. Anthu ambili amene anakhala mnthawi ya m'Cipangano ca Tsopano anamuona Yesu Kristu. Anadziwa malembo a M'cipangano ca Kale bwino, popeza Cipangano cakale cinali Buku lao Lopatulika Buku la Cipangano ca Tsopano linali losalembedwa. Anthu awa anadziwa malonjezo a Mulungu amene analonjeza powelenga buku lao la Cipangano ca Kale. Tsopano, analinkuona ndi maso ao kukwaniritsidwa kwa lonjezano lalikulu la Mulungu. Zoonadi Mulungu nthawi zonse amasunga malonjezano ace.

### YESU - MZATI WA CIPHUNZITSO CA CIPANGANO CA KALE NDI CA TSOPANO

Cipangano cakale ndi ca Tsopano zitenga moyo ndi tanthauzo kucokera kwa Yesu. Tinganene Kuti Cipangano ca Kale ciyembekeza kudza kwa Yesu, ndipo Cipangano ca Tsopano ciyembekeza lonjezano lodalitsidwalo.

### YESU KRISTU, MPHATSO YA MULUNGU

Mphatso ndi Cinthu copatsidwa kucokera kwa munthu wina kupita kwa wina caulere. Nthawi zambili wopatsa

amakhala naco cikondi mu mtima mwace ca pa munthu amene ali kupatsa mphatsoyo. Buku Lopatulika litiphunzitsa Kuti Mulungu anatikonda ife kwambili. Mulungu anatuma mphatso Kudziko lapansi kuti anthu onse akapulumutsidwe kumacimo ao. Mphatsoyo inali Yesu Kristu, Mwana m'modzi yekha wa Mulungu. "Pakuti Mulungu anakonda dziko la pansi kokero, kuti anapatsa mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wokhulupirila Iye asatayike, Koma akhale nao-moyo wosatha." Yohane 3:16.

## PHINDU LA MPHATSO YA MULUNGU

Tinaphunzila sabata latha kuti anthu onse anacimwa. Aroma 3:23. Cimo limapatula anthu ndi Mulungu. Cimo lipatulanso anthu wina ndi mzace. Phindu la kubwela kwa Yesu Kristu ndiko kudzafa pa mtanda cifukwa ca macimo a anthu onse. "Monga Mwana wa munthu sanadzaKutumikiridwa, koma kutumikira, ndikupereka moyo wace dipo la anthu ambili." Mateyu 20:28.

## MPHATSO YA MULUNGU INAIKIDWA KALE PAMENE YESU ASANATUMIDWE

Mulungu akonda anthu onse. Kunali kucokela mcikondi ici cacikulu kuti Mulungu atumize mphatso yace kudziko la pansi la ucimo. Zopeteka zambili zinapatsidwa ndi anthu m'nthawi ya Cipangano ca Kale, koma anali kuganizila kuti kupeleka zoweta kungacotse macimo. Tidziwa kuti nyama zonse za m'dziko sizikhoza kucotsa cimo limodzi. Yesu yekha akhoza kucotsa macimo. Tiyenela kunena kuti anthu amene anali kupereka nyama anadziwa kuti ucimo unayenela kulipidwa. Cimo silikhoza kukhala osalangidwa. Kupeteka kwa nyama, monga nkhosa, kunali kuyamba kwa zopeleka kudziwitsa anthu kuti Yesu adzapetekedwa pa mtanda. Cotero Mau a Mulungu, pothandiza anthu kumvetsa mau ace, aitana Yesu Mwana wa Nkhosa wa Mulungu. "Mwana wa nkhosa, wophedwa kuyambila makhazikidwe a dziko la pansi". Cibvumbulutso 13:8. Monga anthu anali kulingilira za mwana wa nkhosa kuti ampeleke, Yesu apeleka citsanzo podzicha mwana wa nkhosa.

## MPHATSO YA MULUNGU PA MTANDA

Monga tilinkulingilira za imfa ya Yesu pa mtanda, tiyenela kuona cimene cili kucitika mwa cithunzi. Mulungu, pobwela m'thupi mwa Yesu Kristu, anafa cifukwa ca macimo a anthu onse. Mulungu ali Kupeleka njila kwa anthu onse amene ali kutali ndi Mulungu kusonkhanitsidwanso kwa Iye. Tiona pano kuti Yesu Kristu ndiye mphatso yeniyeni, osatinso nyama, "Ndiko kunena kuti Mulungu anali mwa Kristu, alinkuyanjanitsa dziko la pansi kwa Iye yekha, osawelengera zolakwa zao; ndipo anaika kwa ife mau a ciyanjanitso." 2 Akorinto 5:19.

Timanena kuti, 'Mwazi wa Yesu,' kunena imfa yace. "Mwazi wa Yesu mwana wace utisambitsa kuticotsela ucimo wonse." 1 Yohane 1:7. Motero tiona kuti pobvomeleza Yesu Kristu, amene anatifera, macimo athu akhoza kukhulukidwa. "Ngati tibvomeleza macimo athu, ali wokhulupirika ndi wolungama Iye, kuti atikhululukile macimo athu, ndikutisambitsa kuticotsela cosalungama cili conse." 1 Yohane 1:9.

## ZOONA ZITATU ZA YESU KRISTU

1. Yesu analibe cimo. Ngakhale Yesu anayesedwa, sanacimwa. "Pakuti sitili naye mkulu wa ansembe wosatha kumva cifundo ndi zofoka zathu; koma wayesedwa m'zonse monga momwe ife, koma wopanda ucimo." Ahebri 4:15.

2. Yesu anakhala munthu. Ngati wina ayenela kulowa m'malo mwa munthu wina pa mtanda, ayenela kukhala mthupi limodzi ndi maonekedwe amodzi. Ici ndi cimodzi-modzi m'mene Yesu anacitila kwa dziko lonse. "Ndipo Mau anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife." Yohane 1:14.

3. Yesu anali Woyera. Palibe munthu amene anakhoza kupulumutsa anthu ku macimo. Ngakhale kunakakhala kotheka kwa munthu kukhala ndi moyo woona pano pa dziko la pansi, sanakakhoza kupulumutsa ena kumacimo ao. Anali Mwana wa Mulungu amene anapacikidwa pa mtanda ndi kupeleka moyo wace cifukwa ca macimo a dziko la pansi. Yesu atiuza Kuti ali Oyera. "Sukhulupirila kodi kuti ndili ine mwa Atate, ndi Atate ali mwa Ine." Yohane 14:10.